Ubatizo Wa M'madzi

. . .ndipo chirichonse chimene ife timachita chikuyenera kukhala chokhazikika pa Lemba. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. ". . .mpingo wa katolika," iye ananena zimenezo, "ndi kuwona mtima kwako?"

"Chabwino," ine ndinati, "ndine Mkatolika."

Anati, "Inde?"

2 "Chabwino," ine ndinati, "tsopano, monga mwa chiphunzitso cha mpingo wa Katolika, kuti 'Yesu Khristu anakhazikitsa mpingo wa Katolika, ndipo atumwi anali ansembe Ake oyambirira, ndipo Petro anali papa woyambirira.' Izo ziri mogwirizana ndi chiphunzitso cha mpingo wa Katolika, ndipo kuti 'Baibulo ili linalembedwa ndi mpingo woyambirira wa Katolika, chabwino, ndiyeno mpingo wa Katolika uli ndi mphamvu yosintha chirichonse chimene iwo ungafune, chifukwa iwowo ndi mpingowo.'"

3 Ndipo ine ndinati, "Kuyambira masiku oyambirira, kuti, inu nonse munasintha zimenezo. Mwaloweza mmalo kukonkha kapena kutsanulira, mmalo mwa kumiza. Mwaloweza mmalo mgonero mmalo mwa Mzimu Woyera." Ndipo ine ndinati, "Ine ndangokhala mmodzi wa achikatolika achikale amene amakhalabe ndi Chikhulupiriro chapachiyambi, chimene chimaima." Ine ndinati, "Chinthu chachirendo ndi chakuti, kuti Petro, pokhala papa woyamba, anati, 'Palibe mkhalapakati wina pakati pa Mulungu ndi munthu, koma Munthu uja, Yesu Khristu.' Ndipo lero inu nonse muli ndi Maria ndi Cecilia Woyera, ndi mahandiredi a akazi amene anafa, ndi zina zotero, kuti akhale opembedzera. Pali chinachake chimene chinachitika pakati pa papa woyamba ndi papa uyu, mwaona, ngati izo sizimasintha kapena kusokoneza."

4 Ine ndinati, "Ndiye kenanso, kodi inu mumachita chiyani ndi Paulo Woyera, yemwe anali woyera wamkulu wa Mpingo woyambirira wa katolika, amene anati, 'Ngati Mngelo wochokera Kumwamba adzalalikira uthenga wina uliwonse wosiyana ndi uwu umene walalikidwa kale, iye akhale wotembereredwa'?" Ndipo ine ndinati, "Nanga bwanji Yesu Khristu Amene anayambitsa Mpingo wa katolika, anati, 'Ngati munthu aliyense adzachotse Mawu aliwonse mu Baibulo ili, kapena kuwonjezerapo chirichonse kwa Iwo, yemweyo adzachotsedwako, gawo lake, la Bukhu la Moyo'?"

5 Chotero zinthu zonse zimene ife timachita, mwa kuganiza kwanga, monga wokhulupirira Baibulo, ziyenera kukhazikika pa Malemba. Mavumbulutso onse, masomphenya onse, chirichonse, chiyenera kukhazikika modzipereka pa Lemba,

pakuti Amenewo ndiwo maziko amene timapumapo monga PAKUTI ATERO AMBUYE.

6 Mu Malemba, ife sitimapeza pamene iwo anayamba akonkhapo kapena kutsanulira, kapena kuwapatula ana aang'ono mwa njira imeneyo. Koma mu Lemba, ife tikupeza kuti iwo ankabweretsa makanda kwa Yesu, kuti Iye akawadalitse iwo. Ndipo Iye anawanyamula iwo mmanja Ake ndipo anati, "Balolani ana abwere kwa Ine, ndipo musawaletse iwo ayi, pakuti kwa oterewa ndiwo ufumu wa Kumwamba." Ndipo Iye anawadalitsa ana aang'onowo. Ndipo ndiro Lemba lonse limene linalembedwa lokhudza izo. Umo ndi momwe ife timayesera kuti tipitirizire. Tsopano ngati a . . .

7 Monga mu mpingo wa Methodisti, ndi mpingo wa Nazarene, ndi mipingo yina yambiri imene ili ndi- . . . Ine sindikuganiza kuti mpingo wa Nazarene umatero. Mpingo wa Methodisti umatero, ndi ina yambiri kapena oganiza a Evangelical, amene amachita ubatizo wa ana powakonkha iwo.

8 Tsopano, zimenezo ndi zabwino, kachitidwe kalikonse kamene inu mukufuna kuwaperekera iwo, koma kungoti muwone kuti ife sitimaika madzi pa iwo. Ife timangosanjika manja pa iwo, kuyesera kuti titsatire chitsanzo cha Ambuye wathu. Ndipo umo ndi momwe ife timafunira kuti amayi azimvetsera zimenezo, chifukwa chimene ife sitimakonkha madzi pa iwo, chifukwa ife tiribe Lemba lirilonse la izo. Ife tiribe Lemba la kukonkha madzi pa aakulu kapena ana.

9 Chotero, mwanayo wachepa kwambiri kuti abatizidwe. Ndipo ubatizo ndi chiwonetsero chakunjaku kuti ntchito yamkati ya chisomo yachitika. Ndipo mwana sangathe kufotokoza izo, chifukwa sipanakhalepo ntchito iliyonse yachisomo ya mkati, mukuona, chifukwa ndi khanda chabe.

Ndi makolo amene amabweretsa mwana kwa Mulungu Yemwe anawapatsa mwanayo, akumuperekanso iye kwa Iye pomudalitsa. Chotero, ndi momwe ife timagwiritsira ntchito izo apa.

10 Tsopano iwo awabweretsa ana ena kuti adalitsidwe. Ine ndimupempha mlongo ngati iye angatipatse ife poyambira pang'ono pa limba, ya *Abweretseni Iwo Mkati*, Ine ndikukhulupirira, Mlongo Gertie kapena aliyense amene dona wamng'onoyo ali apa.

Ndipo chotero, basi ife tisanachite zimenezo, tiyeni tikhale ndi mawu apemphero kwa amayi ndi anthu amene akubweretsa okondedwa awo.

11 O Ambuye, ndife ndithudi anthu amwayi, kukhala m'dziko limene tikadali nawobe ufulu wa kupembedza, kuti kumene ife tiri ndi boma limene limatiteteza ife ndi kutipatsa cholowa choperekedwa ndi Mulungu ichi; kuti ife sitiyenera kuti tizichita molingana ndi mpingo waboma kapena mtundu wina wa

ulamuliro wankhanza, koma ife tikhoza kubwera kwa Inu mwanjira imene ife tiri otsimikizika mu mtima mwathu. Ife tikupemphera kuti izi zikhale motalika, mpaka Yesu adzabwere, ngati izo ziri mwanjira Yanu yoperekedwa.

12 Ndipo tsopano ambiri a anthu akubweretsa ana awo, tsiku ndi tsiku, ndi sabata ndi sabata, monga Inu mwawaperekera iwo mmanja ndi mchisamaliro cha abambo awo ndi amayi. Iwo akuwabweretsa iwo, Ambuye, kwa ife, ngati ma eledara pano pa mpingo. Ndipo ife, mwa pemphero, tikuwapereka iwo kwa Inu. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mutenge aliyense wa okondedwa aang'ono awa, mmawa uno, ndipo mupatulire miyoyo yawo kwa Inu. Mudalitse mabanja amene iwo akuchokerako. Mulole abambo awo ndi amayi akhale odzipereka kwambiri kwa Inu, kuti anawo aleredwe mmabanja Achikhristu, kuti adzakutumikireni Inu masiku onse a moyo wawo. Titsukeni ife mmawa uno, Ambuye, pamene iwo akubweretsa ana ankhosa osalakwa awa, duwa lenileni la mtima wawo. Koma iwo akufuna kuti iwo akhale ndi Moyo Wamuyaya, ndipo akukupemphani Inu, O Mulungu, kuti muwateteze iwo ndipo muwasunge iwo, ndi kuwatsogolera iwo mpaka atakula msinkhu wokwanira kuti tikhoza kudzalankhulana nawo ndi kuwakopa iwo kuti amulandire Ambuye Yesu ndi kulandira Moyo Wamuyaya. Ife tikuchita izi kwa ulemerero wa Mulungu, malingana ndi Mawu Ake, mu Dzina la Mwana Wake, Ambuye Yesu. Ameni.

13 Tsopano pamene amayi akubweretsa, ndi abambo, akubweretsa ana awo kuno kuti adzadalitsidwe, mlongo aziyimba. Mungowabweretsa anawo ndipo muyime pomwepa pafupi ndi guwa apa, pambali pa aang'ono awa amene adalitsidwa kale. Chabwino.

14 Ukangotha msonkhano uno tikhala ndi msonkhano wa ubatizo. Ndipo pamene iwo akuwabweretsa iwo, ine ndikhoza kulengeza, muwonetsetse kuti mwawabweretsa okondedwa anu kuno tsopano, madzulo ano ikamati sikisi, pakati pa sikisi ndi hafu pasti sikisi iwo akhala akupereka makadi apemphero. Ndipo misonkhano idzakhala ikuyambika, ine ndikuganiza, pa seveni, hafu pasti seveni.

15 Chabwino, bwana. Ingobwerani nawo pafupi ndi anawo, ngati mungathe. Ine ndikuwona amayi akutululutsa kamera yawo apa. Inu mukudziwa momwe amayi amaganizira za ana.

Ndi angati amawakonda ana aang'ono? Oh, mai! Ine ndinkakonda kuwamva aang'ono awa akuimba, *Yesu Amakonda Ana Aang'ono A Mdziko*.

16 Kodi ndinu Mlongo Grimsley? [Mlongo Grimsley akuti, "Inde. Inde, uyu ndi mdzukulu wanga wamng'ono."—Mkonzi]. Mdzukulu wanu. Ine sindikudziwa ngati Meda walowa kale mu tchalitchi, kapena ayi. Ife tinawerenga mu pepala, nthawi yina mmbuyomo, ndipo iye anandiimbira foni ndipo anandiuza ine

kuti Mlongo Grimsley wamwalira kuno mumzinda. Ndipo ife tinadabwitsidwa. Ndiyeno pamene ine ndinadzafika kwathu ndi kudzapita ku tchalitchi Lamlungu limenelo, apa inu munali mutakhala mu tchalitchi. Ndipo ine ndinati, "Chabwino, iye ndi mkazi wamoyo wakufa kwambiri yemwe ine ndinayamba ndamuwonapo." Chotero akuyenera kukhala mlongo wina, Akazi. a Grimsley. ["Uko nkulondola."] Inde, mayi.

17 Tsopano ndikufuna ndimupemphe M'bale Neville ndi ena mwa ma eledara ngati iwo angabwere kutsogolo pa nthawi ino, ndi kudzaima apa mu kudalitsa. Ngati . . . Ena a inu abale otumikira pamenepo, ngati ma eledara, bwerani patsogolo, abale, ndi m'bale.

18 Tsopano, aliyense wa inu amayi ndi abambo, ndi azigogo, mukupereka kwa Mulungu ngale zazing'ono zamtengo wapatali izi zimene Mulungu wakupatsani inu, kuti zidalitsidwe, kuwapereka iwo kwa Mulungu amene anawapereka iwo kwa inu. Chisomo Chake ndi chifundo zikhale nanu, ndiro pemphero langa.

19 Kodi M'bale Collins ali pafupi? Kapena, m'bale, kapena . . . [M'bale Neville akuti, "Ine ndikumuwona M'bale Collins."—Mkonzi]. Muloleni iye abwere kutsogolo ngati iye angatero, kuno chifukwa cha msonkhano uwu, ngati . . . Iye ndi mmodzi wa azibusa othandizira pano, wa mpingowu, ndipo ife tikufuna kukhala naye iye pano ndi pemphero, limodzi nafe, ngati nkotheka.

20 Tsopano, inu mukudziwa, nthawizina . . . Ana awa, iwo sanaphunzirepo izi nkomwe, chotero iwo amangokhala apachiyambi. Ndipo nthawizina amafuula ndi kulira, koma izo zimangowapangitsa iwo kukhala makanda abwino, sichoncho? Chotero, ife sitimazindikira izo. Chotero ngati iwo akulira kapena chirichonse, kumbukirani, zimenezo sizimasokoneza konse. Ine ndikulingalira ana ena omwe anabweretsedwa kwa Ambuye Yesu, anakhala ngati analira pang'ono, nawonso, inu mukudziwa, chifukwa nthawizonse izo zimakhala mwanjira imeneyo. Ana ang'onowo, amasokonezeka akamasunthidwa sunthidwa, ndipo ena akhala atakhala pano mchipinda chotenthachi. Chotero, ife sitimazindikira zimenezo. Chabwino.

Ife tibwera patsogolo.

21 Ndipo kodi dzina lake ndi ndani tsopano? [Mlongo Grimsley akuti, "Etienne Renee Bennett."—Mkonzi]. Tina Renee Bennett. Tina Renee Bennett wamng'ono, agogo ake aakazi amybweretsa iye kuti amudalitsitse. Iye ndithudi ndi mwana wokondeka.

Tiyeni tipemphere.

22 Ambuye, iwo akubweretsa mmanja a wantchito Wanu mwana wamng'ono wokondedwa uyu amene ife tikumupempherera, kumupereka kwa Inu. Mulungu, mdalitseni mwana wamng'ono uyu, ndipo mulole iye akhale moyo ndi

kumadzakupembedzani Inu. Muwadalitse makolo ake ndi azigogo ake. Ndipo, Ambuye, ngati kuli mawa, mulole iye adzakhale wantchito Wanu wamkulu. Perekani izi, Ambuye, pamene ife tikumupereka iye kwa Inu. Mu Dzina la Yesu, mulandireni iye. Ameni. Ambuye akudalitseni, mlongo.

Cynthia Lee Cannard wamng'ono, chidutswa china chokondedwa chaching'ono . . . Mai, iye ndi wamng'ono kwenikweni. Iye ndi wokondedwa? Tiyeni tipemphere.

23 Ambuye, ife tikubweretsa kwa Inu khanda ili, ndipo monga iye wayikidwa kuchokera mmanja mwa okondedwa kupita kwa anga mu kudalitsa koyera, ndi kudzipereka kwa Mulungu . . . Wamng'ono uyu ndi wachichepere kwambiri kuti adziwe, koma okondedwa amubweretsa iye. Mulole iye akhale moyo, Ambuye, ndipo akhale wamphamvu ndi wathanzi moyo wake wonse. Muwadalitse makolo ake, azigogo ake, ndi okondedwa ake onse. Mulole, mu Ulemerero, iwo onse adzasonkhane pamodzi tsiku limenelo pamene ife tidzakomane ndi Inu. Musungeni iye wathanzi ndi wosangalala. Ife tikumupereka iye kwa Inu mu kumudalitsa ndi pemphero, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Ambuye akudalitseni inu.

24 Kodi uyu ndi wanu? Mnyamata wamkulu uyu ndi ndani? Carl Christian Stall, Carl Christian Stall wamng'ono. Iye ndi mdzukulu wa M'bale wathu McDowell. Chotero iye ndi mnyamata wowoneka bwino. Ine ndikupemphera kuti ngati kuli mawa, iye adzakhale mlaliki wa Uthenga. Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu.

25 Ambuye, pamene agogo awa ayika mmanja mwanga thunthu laling'ono la chikondi ili, ine ndikukupemphani Inu, Ambuye Mulungu, kuti Inu mutenge kamwana aka mu chisamaliro Chanu, ndikumulola iye akhale ndi moyo, ndi kukula, ndi kukhala wamphamvu, ndi wathanzi. Mulole, ngati kungabwere mawa, mulole iye adzalalikire Uthenga, umene ife amene tikumupereka iye mmawa uno tikuwukhulupirira. Mulole moyo wake wawung'ono udalitsike kwambiri. Mudalitse makolo ake, azigogo ake, ndi azigogo ake aamuna. Ife tikupemphera kuti madalitso Anu akhale pa iye. Pakuti ife tsopano mwa pemphero la kudzipatula, tikumupereka mwana uyu kwa Inu, O Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana Wanu. Ameni.

26 Wamphamvu wokoma wamng'ono . . . Pepani, inu ndi amake? Mathokozo kwa inu. Ndi wabwino bwanji . . . ? . . . Dzina lake laling'ono ndi ndani? Sheryl Ann Baldwin. Inu ndi amake? Chabwino, ziri bwino. Shirley, ndiwe mtsikana wabwino wamng'ono. Shirley Ann Baldwin wamng'ono. Tsopano, iye ndi wamanyazi pang'ono; iwe ukhoza kudziwa zimenezo. Ndikuganiza kuti amayi ake analinso nawonso . . . ? . . . Ine ndangokumana nawo iwo ine—ine ndikudziwa kuti ndizo . . . Ife tizigwirizana limodzi chomwechi . . . Oh, iye ndi mtsikana

wamng'ono, wabwino, ndikukhulupirira. Iye ndi wokondedwa. Tiyeni tipemphere.

27 Ambuye, tikubweretsa kwa Inu mwana wamng'ono uyu. Chala chake chaching'ono chiri mkamwa mwake, O Mulungu, iye sakudziwa nkomwe chimene chiri lingaliro la tchimo. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudalitse moyo wake waung'ono ndipo muwupange iwo kukhala wolemera komanso wachifumu. Mudalitse amayi ake aang'ono apa, abambo ake, azigogo ake, ndi onse okondedwa ake. Ndipo pamene ife tikumupereka iye kwa Inu mu kupereka kwaulemu kwa pemphero, mumulole Iye akhale ndi moyo, akule, ndipo akakhale wamphamvu, ndi wathanzi, ndipo adzakhale chitsanzo mmasiku ake a umayi wamng'ono kuti adzatumikire Ambuye Yesu. Perekani izi, Ambuye. Ine ndikukhulupirira ndi ana aang'ono otere amene Inu munaika manja anu pa iwo ndi kuwadalitsa. Ife tikupempha izi kwa ulemerero wa Mulungu, pamene ife tikumupereka iye, ndi kumuyeretsa iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Tsopano, ine ndikuganiza iwe ndiwe mtsikana wamng'ono wokoma, wamanyazi, koma wokoma. Mulungu akudalitseni inu. Zabwino zonse chifukwa cha mwana wabwino.

28 Tsopano, mwina kalekale, ine ndikanamunyamula mtsikana wamng'ono monga chonchi. Dzina lako ndi ndani? [Mlongo akuti, "Sharon Diane Bayle."—Mkonzi]. Ine . . . Pachibale ndi wina uja? Uh-huh. Bayle, pafupi kwenikweni. Ine ndikufuna inu nonse mumuwone mtsikana wamng'ono uyu, chifukwa iye ndi kanthu kakang'ono kokoma kwambiri. Ine ndichita kumunyamulira iye mmwamba pang'ono pokha. Mtsikana wamng'ono wokongola kwambiri . . . Ine ndikuganiza kuti anali aang'ono ngati awa amene Yesu anawasanjika manja Ake. Manja athu ndi osayenera bwanji. Koma ngati mungayang'ane manja oyenera, inu simungawapeze iwo. Ndife osayenera, koma ife timatenga lonjezo Lake kudzera mchisomo. Dzina lake kachiwiri? Sherry Diane Bayle. Tiyeni tipemphere.

29 Ambuye, ife tikumubweretsa mwana uyu kwa Inu, wokoma, wokongola. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudalitse moyo wake waung'ono. Mulole iye akhale moyo kuti adzakhale mkazi wamphamvu wodzaza chisomo ndi mphamvu. Mulole iye adzakhale ndi malo mu nkhani yayikulu ya chiwombolo kuti adzachite chinachake cha Ufumu wa Mulungu. Adalitseni amayi ake aang'ono, abambo, azigogo, ndi onse okondedwa ake. Ndipo ngati inu mungamukhalire moyo iye . . . mpaka tsiku lake, mulole iye adzakhale wantchito Wanu. Tsopano, ife tikumupereka iye kwa Inu mwanjira ya kumudalitsitsa kuti apatulidwe, mwanjira ya pemphero, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni. Akudalitse iwe, wokondedwa, mtsikana wamng'ono wokongola, wabwino.

30 Iye adzakhala mtumiki nayenso? Chabwino. Ndipo dzina lake ndi ndani? John Michael Daulton. Tsopano, inu mukudziwa ine ndiri ndi wolishya wamng'ono uko pafupifupi usinkhu wako, John Michael wamng'ono. Chabwino, ziri bwino. Abambo ake apa ndi mtumiki, ine ndikukhulupirira ndiko kulondola. Inu simunali mtumiki wa Baptisti? Membala wamba wa mpingo wa Baptisti. Uko nkulondola. Tiyeni tipemphere.

31 Ambuye, ife tikubweretsa kwa Inu mnyamata wamng'ono uyu. Sindikudziwa chimene ndanyamula mmanja mwanga. Mayi akenso samadziwa pamene iye anabadwa, ndipo manja ake aang'ono anasisita nkhope yake, kapena ya abambo amene anakweza pachifuwa pawo kuti adziwe kuti ali ndi mwana wamwamuna. Mulungu, ine ndikupemphera kuti mwana uyu akhale kwa ulemu ndi ulemerero wa Yesu Khristu. Ife tikumubweretsa iye kwa Inu tsopano mu kudalitsitsa ndi pemphero la kudzipatula, kuti Inu muwugwiritse ntchito moyo wake wawung'ono kwa ulemerero Wanu. Pakuti ife tikumupereka iye kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Akudalitseni inu. Mnyamata wabwino . . .

32 Mnyamata wamng'ono uyu? Oh, kodi uyu ndi mlongo Daulton? Robert Anthony. Mlongo Daulton. Chabwino, ndine wokondwa kukumana nanu, Mlongo Daulton. Ine ndinkamudziwa bwino mwamuna wanu; ine ndikuganiza kuti ndinakuwonanipo. Uyu ndi Robert Lee? Chiyani? Robert Anthony. Chabwino. Oh, mukuti, mai! Tizidutswa ta Kummwera sitinachite *izo* kwa iye. Iye ndi mnyamata wabwino, mnyamata wowoneka bwino. Tiyeni tipemphere.

33 Ambuye, ife tikubweretsa kwa Inu mnyamata uyu kuti adalitsidwe, amene amayi amubweretsa iye ndi abambo. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu muwupatule moyo wake wawung'ono, Ambuye, ku ntchito Yanu. Mulole iye akhale moyo ndikudzakhala mwamuna wopambana, wamphamvu, mwathupi, mwauzimu. Perekani izi, Ambuye. Ndipo tsopano, ife tikumupereka iye kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu. Ameni.

Zabwino zonse kwa inu chifukwa cha anyamata awiri abwino. Ndipo ine ndikuyembekeza kuti awiri onsewo ndi alaliki, ngati Ambuye akachedwa.

34 Apa pali mnyamata wina. Inu mukhoza kudziwa kuti ndi mwana wabwino, mmene iye waligawira tsitsi lake. Dzina lake ndi ndani? Robert Samuel Bates. Tsopano, ine sindikudziwa. Iye ndi wolemera ndithu. Hmm, mai! Robert Samuel Bates, mnyamata wabwino. Tiyeni tipemphere.

35 Wokondedwa Mulungu, ife tikubweretsa kwa Inu mnyamata uyu, ndipo powona kuti iye akuyandikira zaka za mmatini. Oh, misampha imene satana watchera kwa mnyamatayu. Ilambalaleni iyo, Ambuye. Mulole mwanayu asadzayende mnjira

yosalungama, koma mulole pemphero lomudalitsitsa mmawa uno, ndi chikhulupiriro cha makolo limodzi nafe, zipangitse moyo wake waung'ono kuti ukondowezekere ku Kalvare. Perekani, O Ambuye, kuti iye adzakhale moyo ndi kukula, ndi kudzakhala bambo wamphamvu, wabwino. Ngati icho chiri chifuniro Chanu, muloleni iye adzalalikire Uthenga mawa, ngati kudzakhale mawa. Ife tsopano tikumupereka iye kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu Mwana Wanu. Ameni. Mulungu akudalitseni inu.

36 Amenewo ndi m'bale ndi mlongo? Chabwino, izo ndi zabwino kwambiri. Inu muli bwanji? Tsopano, apa palinso mnyamata wabwino. Dzina lake ndi ndani? Sidney, Simminer, Sumner. Dwight Sumner. Nthawi ina kunali mlaliki wopambana wotchedwa Dwight. Huh? Mlaliki wopambana. Ndani akudziwa limene linali dzina lake? Dwight Moody. Uko nkulondola. Wosaphunzira, wokonza nsapato wamng'ono, koma anatumiza miyoyo millioni kwa Yesu. Mulole Dwight wamng'onoyu adzachite chimodzimodzi. (Ndi iwe apa.) Oh, iye ndi mnyamata wabwino, kamnyamata kakang'ono kowoneka bwino, akuwoneka ngati mlaliki. Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

37 Ambuye, ife tikubweretsa kwa Inu, mnyamata wamng'ono uyu, woikidwa kuchokera mmanja mwa okondedwa kupita ku athu. Ndipo mu kukhulupirira ndi chikhulupiriro mu Baibulo, ndi mwa Khristu wa Baibulo ife tikumupereka mwana uyu kwa Inu, kuti moyo wake udzagwiritsidwe ntchito kwa ulemelero wa Mulungu. Mudalitse nyumba yake, makolo ake, okondedwa ake, ndipo mulole iye adzakhale moyo ndipo adzakhale wamphamvu. Ndipo ngati chingakhale chifuniro Chanu, mudzapange mtumiki mwa iye wa mawa, ngati mawa limenelo liti lidzakhalepo. Koma mmapemphero athu, moonamtima, ndi mapemphero opatulika a iye, ife tikumupereka iye kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Mulungu akudalitseni inu. Ndiwe mnyamata wabwino. Zikomo inu, abale.

Oh, ine sindikudziwa, pali chinachake chokhudza anyamata aang'ono amenewo, chimene chimangokupangitsani inu kumverera bwino. Inu mukudziwa, tiri ndi . . .

38 Ndiri ndi bwenzi wanga wamkazi wamng'ono pano. Iye ndi wamanyazi, anamira pansi nthawi yomweyo. Ndimamutcha iye "Cookie." Iye ndi wochokera uko ku Georgia, kumene ine ndinapitako kukachita tchuthi ndi abambo ake posachedwapa, kupita kukawedza. Ndipo chifukwa chimene ine ndimamutchulira iye Cookie; amayi ake atandikazingira ine nyama za T-bone ziwiri kapena zitatu zathunthu ine ndikafika kunyumba, ndipo ine ndinadya mpaka ine sindimakhoza kudya kenanso, kumeneko ndi kuphika kwabwino kwa Kummwera uko; iye anabwera ndi mabisiketi odzadza mmanja. Ine

ndimayenera kuwadya iwo, inenso. Chotero, ine ndinamutcha iye Cookie. Iye ndi mtsikana wabwino.

39 Ana onsewa, inu nonse mukuwakonda Ambuye? Mai, izo ndi zabwino! Kamodzi mu kanthawi, ine ndimangolalikira kwa ana, inu mukudziwa. Ndi angati anali pano pamene ine ndinanena nkhani yokhudza Mose wamng'ono? Inu mukudziwa, sitima yaying'ono ija, inu mukudziwa, imene khanda laling'ono ili linabisidwamo. Inu mukukumbukira zimenezo? Ndipo nonse munabwera mozungulira guwa ndi—ndipo munadzapereka moyo wanu kwa Ambuye Yesu. Tsopano, lero ife tikukondwerera kuwuka Kwake. Inu mukumukondabe Iye? Nonse a inu amene mumamukonda Iye, kwezani mmwamba manja anu, anyamata ndi atsikana inu pano. Oh, ndizabwino bwanji! Zimenezo ndi zabwino, handiredi peresenti! Ndipo ine ndikukhulupirira zimenezo, nanenso, ndi mtima wanga wonse, kuti iwo amamukonda Iye.

40 Tsopano ife tikubwera pakali pano ku utumiki wa ubatizo; ife sitikudziwa kuti ndi angati amene ati abatizidwe. Ndi gawo la Uthenga. Uthenga wa chiukitsiro unali, "Pitani inu mdziko lonse, ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene akhulupirira ndipo nabatizidwa adzapulumutsidwa; ndipo iye amene sakhulupirira adzawonongedwa. Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo, amene akhulupirira," monga zinawerengedwa mmawa uno kwa ife, kuchokera pa Marko 16. Tsopano ife tiwerenga Malemba ena a—ubatizo wa madzi.

41 Tsopano, pali anthu ambiri, ndi mipingo, imene imakonkha madzi pa anthu. Mipingo yambiri imakhulupirira zimenezo. Ndipo ndi mmenemo, bwanji, izo zonse ziri bwino. Ambiri amatsanulira madzi pa anthu, kungowatsanulira iwo, amawatenga madzi ndi kuwatsanulira pa mitu yawo. Chabwino, ndizo—zonsezo nzabwino, mwaona. Ndi kudzipereka. Ndi—ndi—chiwonetsero cha—cha mawonekedwe akunja kuti ntchito yamkati ya chisomo yachitika. Chotero, ine ndiribe choti ndinene motsutsa izo, mwaona.

42 Koma, mu Malemba, iwo amabatizidwa pomizidwa mmadzi. Chotero, choncho, pokhala kuti ndine mkatolika wa kachitidwe-kachikale, Ine kulibwino ndichite momwe Mpingo wa kachitidwe-kachikale unkachitira izo, inu mukudziwa, mwa kumizidwa, kuphimbidwa paliponse.

43 Yesu anasindikizidwira kutali mwathunthu. Iye anayikidwa pansi mu nthaka, ndipo mwala waukulu unagubuduzidwira pa mandapo. Poikidwa mmanda, Iye ananyamulira machimo athu kutali. Chotero, ife tikukhulupirira zimenezo. Zimene ena amachita, ndi zabwino, ife tiribe zotsutsana ndi iwo. Koma, kwa ifeeni, ife timakhulupirira mu kumizidwa.

44 Ndipo tsopano ife timapanga kumiza uku molingana ndi Ziphunzitso zoyambirira za atumwi za Mpingo. Ena a iwo amene amamiza, komabe lero, anachokako ku—mwambo woyambirira wa Chikhulupiriro cha atumwi. Pachiyambi, ubatizo woyambirira umene unabatizidwapo itachitika Pentekoste, unali kubatizidwa mu Dzina la "Ambuye Yesu Khristu." Ndipo ubatizo uliwonse pambuyo pake umatero, mmodzi aliyense, ankabatizidwa mu Dzina la "Ambuye Yesu Khristu."

45 Ndipo ena a anthuwo, ife tiwerenga mu kamphindi, omwe anabatizidwa pomizidwa, ndi Yohane M'batizi, ankatero ku kulapa, osati ku chikhululukiro cha machimo. Ndipo iwo anachita kubwera ndi kudzabatizidwanso kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti alandire Mzimu Woyera.

46 Tsopano, lero, ife taloweza mmalo Machitidwe, kapena, Mateyu 28:19, pamene Yesu Khristu anaulamulira Mpingo Wake, "Pitani inu chotero ku mafuko onse, kukawaphunzitsa iwo kuti asunge zinthu zonse zimene Ine ndakuphunzitsani inu; kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Petro, atapita masiku teni, anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo, palibe, palibe aliyense mu Baibulo amene anabatizidwapo mu dzina la "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Izo mulibemo mu Malemba, palibe amene anabatizidwapo.

47 Ndiyeno wina akhoza kunena tsopano, mwaona, izo zinadzozedwa ngati mpingo wa Katolika, chikhulupiriro cha-. . . , kapena, *Mfundo Za Chikhulupiriro Chathu*, mu bukhu la Katolika, mfundo za chikhulupiriro cha Katolika, zimanena kuti, "Achiprotestanti amazindikira ubatizo wathu." Dayosisi ya Katolika, mu. . . pafupifupi sikisi-. . . zaka za mazana fortini, anabatiza munthu, pomukonkha iye, mu dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera," koma palibepo Lemba la izo. Mpingo; Wesile anatulukamo, ndi Lutera, ndi chinthu chomwecho, kuchokera ku mpingo wa Katolika. Ena a iwo amanyamulabe katekisimu wa Katolika, ena amanyamulabe Kachikhulupiriro ka Atumwi, ndi zina zotero, omwe anatuluka mu mpingo wa Katolika. Chimene, ngati Mulungu wapanga Mkhristu kuchokera mwa munthu, monga choncho, ine ndiribe kanthu koti ndinene motsutsa izo. Inu mukumvetsa, mwaona.

48 Koma, kwa ine, ndikuyenera kukhala wa katolika wa kachitidwe-kachikale, ndikuyenera kukhala ndi chimene Mpingo woyambirira unkachita. Ndipo ine ndikuyenera kumabatiza monga momwe Mpingo woyamba unkabatizira, mu Dzina la "Ambuye Yesu Khristu." Ndipo tsopano ife timayesera kuti tisunge izo.

49 Tsopano, kuti ine ndinene ichi, mu Mateyu 28:19, Yesu anati, "Pitani inu chotero, mukaphunzitse mafuko onse,

mukawabatize iwo mu Dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera."

50 Chabwino, tsopano, mmodzi wa iwo, Iye sananene, "mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, mu dzina la Mzimu Woyera." Iye anati, "mu Dzina," limodzi. Ophunzira opambana monga Scofield ndi iwo, ndi Achigriki apachiyambi, onse, ndipo mu . . . kumasulira konse, ndi "mu Dzina." Osati "mayina" kapena "mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana." Ndi "mu Dzina" la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera!

51 Chabwino, "Atate" si dzina, ngakhalenso "Mwana" si dzina, ndipo ngakhalenso "Mzimu Woyera" si dzina. Iwo ndi maudindo amene amapita ku Dzina limodzi. Mwaona, pali Dzina limodzi! Ndiye ngati . . . Vumbulutso limene ife tikuyesera kuti tiribweretse kwa inu ndithudi likuyenera kuti linali vumbulutso lomwelo limene atumwi anali nalo pamene iwo anayima pafupi ndi Iye, akumumvetsera Iye akupereka kulamula kumeneko.

Winawake anati, "Chabwino, ine sindikusamala zomwe atumwi anachita, Yesu ananena *izi*!"

52 Ngati atumwi sanamumvere Iye, ndiye kuti Malemba akulakwitsa. Inu mukuyenera kuwapanga Malemba kukhala angwiro, apo ayi iwo si kanthu. Iwo ndi Mawu aliwonse olondola kapena palibe aliwonse a Iwo amene ali olondola. Ine sindikudziwa chomwe chingakhale cholondola ngati Iwo onse si olondola. Ngati gawo la Iwo silodzozedwa, ndiyeno ena onse a Iwo sangakhale. Koma palibe kutsutsana m'Malemba.

53 Chotero ngati Petro anati, "Lapani, ndipo mubatizidwe, aliyense wa inu, mu Dzina la Yesu Khristu," ndipo onse pambuyo pake anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo Yesu anati, "Pitani, mukabatize mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera," ndiko kutsutsana kochepa, zimawoneka chomwecho; koma sichoncho, ngati inu mukanangodziwa.

54 Kumbukirani, "Malemba anabisidwa mmaso mwa anzeru ndi ophunzira." Kodi inu mumadziwa zimenezo? "Ndipo kuti adzawululidwa." Malemba samadzitsutsa Okha; Iwo amangodzilengeza Okha.

55 Tsopano, ngati inu mungabwerere mmbuyo. Ngati inu mumawerenga nkhani, monga ngati mukanati, "John ndi Mary anakhala osangalala kuyambira nthawi imeneyo." Monga ena a inu, ndife tonse olakwa kuti timawerenga nkhani. Ndipo ngati inu simumadziwa kuti John ndi Mary anali ndani, chinthu chokhacho chimene mungachite ndikubwerera koyambirira kwa bukhulo, ndi kukawerenga yonseyo ndi kukapeza kuti John ndi Mary anali ndani.

56 Ngati Yesu anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu "Dzina" la Atate, Mwana, Mzimu Woyera; ndipo Atate si dzina, ndipo Mwana si dzina, ndipo Mzimu Woyera si dzina; kulibwino ife

tibwerere mmbuyo ndi kukapeza Yemwe "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera" ali, ndi chimene Dzina Lake liri.

57 Chotero ngati inu mungatsegule ndi ine, pa mutu wa 1 wa Mateyu, monga inu mungachitire ndi Bukhu lirilonse. Ilo linati tsopano, kuyambira ndi mabadwidwe, Ilo linati:

> *Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Pamene . . . amayi ake Mariya anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, . . .* anatomeredwa, mwakuyankhula kwina.

58 Tsopano ine ndikufuna kuti ndikuwonetseni inu momwe ziliri. Penyani, ife tinena kuti *uyu* ndi Mwana Yesu, *uyu* ndiye Atate, *uwu* ndi Mzimu Woyera. [M'bale Branham akuwonetsa zinthu zitatu monga zitsanzo—Mkonzi]. Tsopano, aliyense akudziwa, ndipo Yesu ananena kuti Mulungu anali Atate Ake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."] Ife tikuyenera kutero! Atate a Yesu Khristu anali Mulungu. Tsopano ine ndikubwereza Lemba, Mateyu 1:18.

> *. . . kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Pamene . . . amayi ake Mariya anatomeredwa ndi Yosefe,* iye *asanafike, iwo pobwera pamodzi, anapezeka ali ndi mwana mwa Mzimu Woyera.*

Ndiye ndi uti mwa *awa* amene ali Atate Ake?

> *Ndipo iye adzabala* mwana, *ndipo* iwo *adzamutcha dzina Lake YESU: . . .* Zindikirani, iye anali . . .

> Ndipo pamene *Yosefe mwamuna wake, pokhala munthu wolungama . . .* posafuna *kuti amunyazitse poyera, anaganiza kuti amusiye iye* mwamseri pa chifukwa ichi.

> *Koma* pamene *iye analingalira pa zinthu izi, taonani, mngelo wa Ambuye anawonekera* kwa *iye mu loto,* ndi *kuti, Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope kudzitengera wekha* mkazi wako, *Mariya mkazi wako: pakuti icho chimene chiri mwa iye ndi cha Mzimu Woyera.*

59 Bwanji, Mulungu angakhale bwanji Atate Wake, ngati Mzimu Woyera uli Atate Ake? Iye akanakhala ndi abambo awiri, ndipo Iye akanakhala mwana wamtundu wanji? Palibepo awiri. Mzimu Woyera ndi Mulungu ndi chinthu chomwe chomwecho. Mukuona?

> *Ndipo iye adzabereka mwana wamwamuna, ndipo* iwo adza*mutcha dzina lake YESU: . . .*

> *. . . zonse izi zinachitika, kuti zikakwaniritsidwe zimene zinanenedwa ndi Ambuye mwa mneneri, kuti,*

> *. . . namwali* adzaima ndipo adzabala *mwana, . . . ndipo* adzatchedwa *Emmanuele, chimene chiri* (chiyani?) *Mulungu nafe.*

60 Tsopano, *apa* pali Mwana. Pa tsiku la ubatizo Wake mu Yordani, Yohane akuchitira umboni akuwona Mzimu wa Mulungu, ngati nkhunda, ukubwera ndi kudzakhala pa Iye. Yesu anati, "Si Ine amene ndikuchita ntchitozo; ndi Atate Anga amene akukhala mwa Ine."

61 Tsopano, "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera" ali ndi Dzina limodzi, maudindo atatu amenewo, ndipo Baibulo kodi linati Dzinalo linali chiyani? [Winawake akuti, "Yesu."—Mkonzi]. Yesu! Chotero limenelo likuyenera kuti linali vumbulutso limene atumwi anali nalo, pakuti umo ndi mmene iwo ankabatizira. "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera" si dzina, palibe limodzi la ilo limene liri mayina. Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera ndi "Ambuye Yesu Khristu." Ndiro Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera.

62 Tsopano ine ndiwerenga Malemba ena ife tisanabatize. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge, poyamba, pa chochitika choyamba cha ubatizo wammadzi, ndipo izi zikupezeka mu Machitidwe mutu wa 2, Petro pa Tsiku la Pentekoste. Iye anakhala akulalikira.

> Ndipo *pamene iwo anamva izi, analaswa mu mtima mwawo, ndipo anati kwa Petro ndi. . . atumwi enawo, Amuna ndi abale, kodi ife tichite chiyani?*
>
> *Kenako Petro anati kwa iwo, Lapani, ndipo batizidwani aliyense wa inu mu dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.*
>
> *Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu,* kwa iwo amene ali *kutali, ngakhale ochuluka amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitane.*

63 Kenako nthawi yotsatira imene ife tiri ndi ubatizo umene unachitika, ndi pamene Filipo, patapita masiku awiri, anatsikira ku Samaria. Iwo anali Ayuda, ndiyeno pamene. . . Pali mitundu itatu yokha ya anthu pa dziko lapansi, ndiwo anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti; Ayuda, Amitundu, ndi (theka Myuda ndi Wamitundu) Asamariya. Pamene Filipo anapita ndi kukalalikira kwa Asamariya, izi ndi zomwe zinachitika. Simoni mmodzi uyu, wamatsenga, ankawalodza anthu mwa matsenga.

> *Koma pamene iwo anakhulupirira Filipo akulalikira zinthu* zokhudza u*fumu wa Mulungu,* mu *dzina la Yesu Khristu, iwo anabatizidwa, amuna ndi akazi omwe.*

64 Nthawi yotsatira imene ubatizo ukunenedwapo, ukupezeka mu Machitidwe 10:44 mpaka 48, kunyumba ya Korneliyo, Wamitundu. Pali Ayuda ku Yerusalemu, Filipo ku Samariya, ndipo apa pali Petro ndi Amitundu.

Ndipo *pamene Petro anali chiyankhulire mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa . . . iwo amene anamva mawu.*

Ndipo iwo a mdulidwe (Myuda) *amene anakhulupirira anazizwa, ochuluka amene anabwera ndi Petro, chifukwa . . . pa Amitundu panali* nawonso *patsanuliridwa mphatso ya Mzimu Woyera.*

Pakuti iwo anawamva iwo akuyankhula ndi malirime, ndi kumukweza Mulungu. Kenako Petro anayankha,

Kodi munthu angaletse madzi, kuti awa asabatizidwe, . . .

Ndipo iye anawalamulira iwo . . .

. . . ndani amene *walandira Mzimu Woyera monganso ife?*

Ndipo iye anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu dzina la Ambuye. Mukuona? Anawapempherera iwo . . .

Nthawi yotsatira imene ubatizo ukunenedwa, ndi mu Machitidwe 19, pamene iwo anabwera kwa ophunzira a Yohane. Uyu ndi Paulo, tsopano mvetserani mwatcheru, Machitidwe 19.

Ndipo kunachitika, . . . pamene Apolo anali ku Korinto, Paulo atadutsa ku magombe akumtunda kwa Aefeso: iye akuwapeza *ophunzira ena,*

Ndipo, *anati kwa iwo, . . .*

Tsopano taonani. Iwo anali ophunzira. Iwo anali okhulupirira, Akhristu.

Iye anati kwa iwo, Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni? Ndipo iwo anati kwa iye, Ife sitinamve konse zoti kuli Mzimu Woyera.

Mvetserani chimene iye anafunsa. Mvetserani funso lofunika ili limene mtumwi uyu anafunsa. Mukuona?

Ndipo iye anati kwa iwo, Nanga munabatizidwa kwa *chiyani? Ndipo iwo anati* kwa Iye, Pansi pa *ubatizo wa Yohane.*

65 Tsopano ine ndingalingalire mmawa uno, ngati mwina, aliyense wa ife anabatizidwa ndi munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu Khristu, ife tikhoza kuganiza kuti ubatizo wathu unali wotetezeka bwino lomwe. Kodi inu simungaganize chomwecho? Koma apa pali Paulo, akuti sichoncho. Mu dzenje lomwelo la madzi, ndi munthu yemweyo amene anamubatiza Ambuye wathu, Paulo akutsutsa ubatizo umenewo tsopano chifukwa iwo sunali mu Dzina la Yesu Khristu. Tsopano mvetserani.

Ndipo iye anati kwa . . . Kodi ndiye munabatizidwa kwa chiyani? . . .

Tsopano ngati inu mukufuna kuti muziyang'ane izo mu Chigriki, iyo inati, "Kodi munabatizidwa *motani*?" Mukuona?

> . . . *Ndipo iwo anati* kwa iye, *Ku ubatizo wa Yohane.*
>
> *Ndiye Paulo anati, Yohane indetu ankabatiza- . . . ubatizo wa kulapa, kunena kwa anthu, kuti akhulupirire pa iye* amene wabwera, *ndiko kuti, pa Yesu Khristu.*

Zindikirani, gulu lomweli linabatizidwa mu Yordani, ndi Yesu Khristu.

> *Pamene iwo anamva izi, iwo* anabatizidwanso, *anabatizidwa mu dzina la Ambuye Yesu* Khristu.
>
> . . . *Paulo* ataika *manja ake pa iwo, Mzimu Woyera unadza pa iwo; ndipo iwo anayankhula ndi malirime, ndipo ananenera.*

66 Tsopano, Paulo yemweyu akunena apa, mu Bukhu la Agalatiya. Ichi ndi chifukwa ine ndikukhalabe pa iyo. Agalatiya, mutu wa 1 ndipo ndime ya 8. Mvetserani. Ine ndiyambira pa—pa ndime ya 6. Kuyankhula kwa Agalatiya.

> *Ndikudabwa kuti mwachotsedwa* mwamsanga *kwa iye amene anakuitanani inu* ku *chisomo cha Khristu kupita ku uthenga wina:*
>
> *Umene si winanso; koma pali ena amene amakusautsani, ndi* . . . kuletsa *uthenga wa Khristu.*
>
> *Koma ngakhale ife, kapena mngelo wochokera kumwamba,* (ameneyo akhoza kukhala wansembe, papa, mlaliki, chirichonse chimene chingakhale) . . . *ngakhale ife, kapena mngelo wochokera kumwamba, angalalikire uthenga wina uliwonse kwa inu kusiyana ndi umene ife talalikira kwa inu, iye akhale wotembereredwa.*
>
> Ndipo *monga* . . . Ndipo *tinanena kale, chotero* tsopano ine ndikunena *kenanso, Ngati munthu aliyense alalikira kwa inu uthenga wina wosiyana ndi* umene inu *mwawulandira, iye akhale wotembereredwa.*

67 "Ngati ife tichotsapo Mawu amodzi mu Baibulo," Chivumbulutso 21 kapena 22, ndipo, "kapena kuwonjezera chinthu chimodzi kwa Iwo, modziwa, zomwezo zidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo, kwa ife." Chifukwa chake, Izo ndikutsimikiza kwanga.

68 Osati kunyozetsa anthu amene akufuna kuti akonkhedwe, kutsanuliridwa kapena kumizidwa, mwa "Atate, Mwana, Mzimu Woyera," ndizo mwadala kwa inu, m'bale wanga wokondedwa, mlongo. Ine sindingatsutsane nanu, ine basi . . . Iwe ndi—ndiwe wa ntchito wa Mulungu.

69 Koma, kwa ine, ine ndikuyenera kukhala wokhulupirika ndi woona ku Baibulo. Chotero, Paulo anawalamulira anthu,

amene anali atabatizidwa mwanjira ina pambali pa Dzina la "Yesu Khristu," ndipo anawakakamiza iwo kuti abwere ndi kudzabatizidwanso, mu Dzina la Yesu Khristu. Kuti ndilalikire Uthenga womwewo, ine ndikuyenera kuchita chinthu chomwecho, kuwakakamiza ndi kuwachondelera anthu. Musasiye konse mpingo wanu; mukhale ndi m'busa wanu, muzichita chirichonse chimene mungathe mu mpingo wanu, koma mutsatire malangizo a Baibulo! Chotero ife tikukhulupirira, mmawa uno, kuti Yesu akubwera. Ndipo ine ndikadzaima tsiku limenelo . . .

70 Tsopano, mwinamwake bukhu la kachikhulupiriro likhoza kukhala labwino bwino. Ine sindingalinyozetse ilo. Ilo likhoza kukhala labwino bwino. Koma, ndipo mwinamwake mpingo wa Katolika uli ndi ulamuliro umenewo. Ine sindikudziwa. Ndipo ngati inu Akatolika pano, ndipo inu mukuganiza kuti mpingo wanu uli ndi ulamuliro umenewo, *Ili* iwo amati ndi Bukhu lawo lapachiyambi. Chotero nchifukwa chiyani mumatenga zimene munthu wina wamakono ananena, pamene Khristu, Woyambitsa mpingo wanu, analamula Izi, pamene papa wanu woyamba analamulira *Izi*? Tiyeni titsatire Baibulo, pakuti ine ndikukhulupirira Icho ndi Choonadi!

71 Tsopano pamene ife tikukonzekera, ndikufuna iwo amene akufuna kuti abatizidwe abwere kutsogolo ndi kudzayima apa, kotero ife tithe kuliwonetsa dziko lapansi kuti timakhulupirira izi.

> Yesu pokhala moyo, Iye anatikonda ife. Pakufa, Iye anatipulumutsa ife.
> Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo athu kutali.
> Powuka, Iye analungamitsa mwaulele kwanthawizonse.
> Ndikukhulupira tsiku lina Iye akubwera, ndikuyembekezera tsiku la ulemerero limenelo!

72 Ndipo inu mukubwera mmawa uno kudzavomereza zimenezo. Tchimo lija limene ine ndinalalikira mmawa uno, machimo a dziko lapansi, atsutsidwa ndipo aphedwa, ndipo simulinso wantchito wa chinthu chimenecho, koma icho ndi chakufa. Ndipo inu mukubwera kudzayikidwa mmanda mu Dzina la Iye amene anakuferani inu, ndipo anakupherani inu tchimo, ndipo anauka kuti mulungamitsidwe. Ndipo inu muli amphumphu, mwa Iye; osati mu mpingo, osati mu Branham Tabernacle, osati mu mgwirizano. Koma inu ndinu amphumphu ndi otetezeka mwa Yesu Khristu!

73 Tiyeni tipemphere. Ambuye, izi nthawi zina zimawoneka ngati zovuta, pakuti ine ndikudziwa kuti ndiri ndi abwenzi ofunika pano a chikhulupiriro cha Katolika, ndi ena a

Methodisti achi Wesile, ndipo, mosakayika, ambiri okhulupirira mowonjeza autatu.

74 Ife tikukhulupirira, Ambuye, kuti "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera" ndi Mulungu yemwe yemweyo, koma maudindo atatu amene Mulungu Wakumwamba anatumikiriramo: nthawi ina kwa Ayuda, mu Utate; kena mu thupi, monga Umwana; ndipo tsopano mu Mzimu Woyera, mu Mpingo. Osati amulungu atatu, ife sitimakhulupirira, Atate; pakuti Inu simungakane Mawu Anu Omwe, pamene kulibe Mulungu wina kupatula Inu. Inu munati, "Ine ndine Yehova Mulungu wanu, musakhale nayo milungu ina." Ndipo ife tikukhulupirira, Ambuye, kuti Mulungu mmodzi woona uyu anakhala mu nyengo zitatu zosiyana: pansi pa lamulo; pansi pa nyengo ya Chikhristu pamene Khristu anali padziko lapansi mu thupi la mnofu limene linabadwa mwa namwali Maria, anafa, anaukanso, ndipo watiwombola ife, Mpingo; ndipo tsopano, mmawonekedwe a Mzimu Woyera, Mboni ya chiwukitsiro imakhala mmiyoyo yathu. Tikhululukireni ife machimo athu.

75 Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mumudalitse munthu aliyense pano, mosalabadira mpingo wake kapena chipembedzo. Iwo ndi anthu amene amakhala moyo ndipo amadya, ndi kukonda, ndipo akufuna kudzapita Kumwamba. Iwo ali monga ife tonse. Ndipo ife—ife tiri—ife sitikuyesera kuti tinyozetse chirichonse kapena ntchito iliyonse imene aliyense wayigwira mu Dzina Lanu, koma ife tikungoyesera kupereka maneno a chiyembekezo chimene chiri mwa ife, mokhazikika pa Mawu Anu. Mawu Anu ali Choonadi.

76 Chotero ife tikupemphera, Atate, kuti ngati pali ena pano amene Inu mungakonde kuti iwo abatizidwenso, aloleni iwo abwere kutsogolo. Ndipo iwo amene sanapangepo kuvomereza kwa Chikhristu, amene akubwera tsopano kuti adzabatizidwe mu Dzina la Ambuye wawo wowukitsidwa, ndi nthawi yokoma bwanji kupanga izo, mmawa wa Isitara. Nchiyani chimapanga ubatizo? Chifukwa kunali Isitara. Perekani, Ambuye, kuti aliyense amene atabwere, adalitsike ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera, monga momwe iwo akufunira. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

77 Tsopano, iwo amene abwerera ubatizo, kodi mungaimirire pa mapazi anu? kuti tidziwe bwino lomwe kuti ndi ndani amene atabatizidwe. Pakhala wani, thuu, firii, foro, faifi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni, leveni, thwelofu, sartini, fortini, fifitini, sikisitini, seventini, eyitini. Eyitini a iwo. Chabwino. Ine ndiri ndi yanu kumbuyo uko, mlongo kumbuyoko.

Tsopano ine ndikanakonda nonsenu, ngati inu mungayende kubwera patsogolo apa mphindi chabe. Inu mutero?

Inu mungatiimbire ife, mlongo, "Ine ndikumumva Mpulumutsi wanga akuitana"? Mwakachetechete mmene mungathere, pang'onopang'ono.

78 Ndipo pamene ine ndikuwona, akutsika pa mzerewu, powadziwa anthu, ine ndikuwona anthu ochokera kunja kwa mzinda, ochokera ku mipingo imene ingaganize kwenikweni kuti ine ndachoka pamzere pang'ono, powabatiza anthu . . . (Kodi inu mungasunthire njira *iyi* pang'ono pokha, abale, kuti awa kumbuyo apa . . . ? Eya.) . . . powabatiza iwo mu Dzina la Ambuye Yesu. Koma ine ndithudi ndayesetsa kuti ndizipange izo momveka basi mmene ine ndikudziwira kuti ndingazipangire izo. Mukuona?

Tsopano, ili ndi gulu labwino la anthu. Ine ndikufuna inu nonse kuti mutembenukire kwa gulu, monga *chonchi*. Chabwino.

79 Anthu awa amene ayima apa, akubwera pa maziko akuti akhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, kuti Iye anali . . . anazunzika pansi pa Pontiyo Pilato, ndipo anapachikidwa pa Kalvare, anafa, anaikidwa mmanda; anawuka tsiku lachitatu, anagonjetsa imfa, gehena, ndi manda, ndipo anakwera Mmwamba, akukhala pa dzanja lamanja la Ufumu, kuti adzipanga kupembedzera pa kuvomereza kwawo. Iwo awonetsera tsopano kwa inu kuti akukhulupirira izi mozama ndi mtima wawo wonse, ndipo avomereza machimo awo pamaso pa Mulungu, ndipo atsimikizika kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu, ndipo amuvomereza Iye ngati Mpulumutsi wawo wawo.

Ngati izo ziri chomwecho, kwezani manja anu, nonsenu amene mwayima mozungulira monga choncho. Ingokwezani iwo. Uh-huh.

80 Chotero, ena a iwo akhala ali Akhristu kwa nthawi yaitali. Ena a iwo anabatizidwa mu dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera. Ndipo iwo atsimikizika lero kuti—kuti Lemba ndi njira ya atumwi ya ubatizo ndi mu Dzina la "Ambuye Yesu Khristu." Ndipo iwo abwera, akukhulupirira izi, ndipo avomereza izo, ndipo akuzifungatira izi, ndipo adzaganiza kuti ndicho Choonadi chifukwa Lemba limaphunzitsa zimenezo.

81 Ngati oterowo ayima pa mzere, inu mungakweze manja anu? inu amene munabatizidwapo kale ndipo mu . . . mu dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera," ndipo tsopano mukhulupirira mwa "Ambuye Yesu Khristu." Zikomo inu.

82 O Ambuye, Mlengi wa Kumwamba ndi dziko lapansi, Woyambitsa wa Moyo wosatha, apa payima amuna, akazi, anyamata ndi atsikana, amene ine nditi ndiwatsogolere apa ku manda a Isitara awa. O Mulungu, tsikulina, mwinamwake tsiku ili apabe, ine ndikuyenera kuti ndidzayime ndi iwo pa Malo wa Chiweruzo. Ndipo pamene Bwana wamkulu adzabwera mu

zovala Zake zachifumu zopambana; ngati mtumiki wa Uthenga, ine ndikuyenera kudzayima pamaso pa Baibulo lotsegula ili ndi kudzapereka umboni wa chimene ine ndawaphunzitsa anthu. Ine ndikuwopa, Ambuye, ndi mantha, mantha a umulungu, kuti ndingaphunzitse chinachake chimene chiri cholakwika, ndipo kenako zonse zimene ine ndachita zingatayidwire kutali. Pakuti, Inu munati, "Mpaka miyamba ndi dziko lapansi zidzatha, palibe Mawu Anga amodzi amene ati adzathe." Ndipo Inu munati, "Mulole mawu onse a munthu akhale olakwika," ndipo Anu akhale olondola.

83 Chotero, Ambuye, ine ndiri ngati wantchito Wanu mu masiku amene apitawa, ndikuwakakamiza iwo kuti abwere ndi kudzabatizidwa kenanso. Kuti ine ndidzathe kunena zimenezo pa tsiku limenelo, kuti, "Ine ndachita zonse monga momwe ine ndimadziwira kuchita kwake. Pamaso pa kutsutsidwa, ndi chirichonse, koma ndayesera kukhala woona ku Baibulo ili."

84 Perekani, Ambuye, kuti moyo wawo ulemeletsedwe ndi kudalitsidwa, ndipo mulole iwo asasowe kanthu. Mulole Mzimu Woyera ubwere pa aliyense wa iwo amene sanamulandire Iye panobe. Mulole iyi ikhale nthawi ya chiwukitsiro, kuti gulu ili la anthu liwukitsidwe, ndipo mpingo uwu upatsidwe Mphamvu ya Yesu wowukitsidwa. Mutilole ife tizipita kuchoka mu chipinda chino lero, tikuti, "Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu, pamene Iye amayankhula nafe panjira." Perekani izi, Atate. Ngati wantchito Wanu, ndi zinthu zogwirika izi, mmene ife tikupitira patsogolo tsopano kuti timvere Malamulo Anu. Mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana Wanu. Ameni.

85 Tsopano azimayi, ine ndikukhulupirira, mupite mchipinda ichi. Nkulondola uko? [M'bale Neville akuti, "Uko nkulondola."—Mkonzi]. Cha uko kumene kukhale zokonzekera, azimayi a mtchalitchi muno atenge malo awo apa ndi azimayi awa, ku mbali ya dzanja langa lamanja. Amuna apita mbali *iyi*, imene ili mbali ya kumanzere. Ndipo Doc, ngati iye angathe, upititse nyali zazikuluzo mobatiziramo, aliyense azitha kuwona utumiki wa ubatizo. Ndipo M'bale Neville azindiyambitsira ine nyimbo, ngati iwo angathe. Ndipo ife ti. . . [M'bale Neville akuyankhulana ndi M'bale Branham]. Ndiye ikani chimenecho pafupi. [Malo opanda kanthu pa tepi].

86 Kuti iye anapita ku. . . kumusi ku Corydon, kwa mkazi amene sanali kanthu koma mthunzi wa mkazi, ali ndi khansa. Ndipo anakamusewerera iye tepi, ya umodzi wa misonkhano, ndipo mkaziyo wawomboledwa kwathunthu, ali pabwalo uko, akusesa masamba. Madokotala sakupeza kanthu kalikonse ka khansa yake.

87 Masiku pang'ono apitawo, mzimayi anadzakhala apa, kumene ine ndinafunsa ndipo ndinati, mwa osonkhana apang'ono, "Ife sitinapeze mwayi wopereka makadi a pemphero,

chotero ine ndingofunsa, ndi angati muno amene sanakhalepo konse mu misonkhano yanga?" Ambiri anakweza manja awo. Mzimu Woyera wawukulu unayenda pa malopo ndipo unayamba kuzindikira malingaliro a anthu ndi chimene iwo akuyenera kuchita. Panali khanda laling'ono litakhala pamenepo lochokera kwinakwake mu Georgia, ali ndi nthenda ya khungu, chibadwireni chake. Masiku awiri kenako, winawake anadzayimba, kapena masiku pang'ono kenako, ndipo anati, "Nthenda ya khunguyo imachoka pa mwanayo."

88 Dona atakhala apa, amapita ku opareshoni, ali ndi khansa yaikulu mmbali mwake, imene inali yoti akapange opareshoni, Lachiwiri lotsatira. Limenelo linali Lamlungu. Iye anabwera ndi chidakhwa, anali chomwecho, Rosella Griffith. Ndipo pamene mkazi uyu anadzabwera, ndipo Mzimu Woyera unayamba kumuuza iye yemwe iye anali ndi kumene iye amachokera, Iwo unati, "Inu mukhoza kuganiza kuti Rosella watiuza ife zimenezo." Kenako Mzimu Woyera unapita ndipo unakamutenga mwana wake kuchokera mwa omvetsera, ndipo unanena za mwanayo, ndipo unati, "PAKUTI ATERO AMBUYE, chotupa chimenecho chachokapo."

89 Ndipo Lachiwiri mmawa pamene iye anadzapita kuti akayezedwe, kapena ku opareshoni yake, pamene akatswiri onse, foro a iwo, ine ndikukhulupirira, anasonkhana pamodzi. Iwo anayamba kuchigwira chotupacho, ndipo icho panalibepo pamenepo. Iwo anamuyika iye pa x-ray, ndipo anayitanapo adokotala ena, ndipo anamuveka zovala zake ndi kumutumiza kwawo, "Mulibemo kalikonse mmenemo."

Mulungu akadali Mulungu! Musataye chikhulupiriro, muzingokhulupirirabe. Chabwino.

90 Nonsenu mundipempherere ine pamene ife tikupita ku California, ku misonkhano; muchita zimenezo tsopano? Ife tikuyenera kukhala titapita, pafupifupi, pakati pa masiku teni kapena fifitini, ku Angelus Temple, kuyambira pa firii.

91 Kenako ife tidzapita, kuchokera kumeneko, usiku umodzi ndi anthu achi Spanish, mu holo ku Los Angeles, pa sikisitini. Seventini, eyitini ndi naintini, ife tidzakakhala ku bwalo la asirikali ku San Diego.

92 Ndipo kenako ife tidzapita tikachoka kumeneko, tidzapita ku San Jose. Amenewo ndi mailosi sarte kuchokera ku Oakland, chifukwa ife sitinapeze malo amene ife tinali nawo chaka chatha. Iwo akuchitako masewera a chipale kumeneko. Ndipo ife tapeza mabwalo achiwonetsero, kumene kuti kudzakhale pafupifupi, ine ndikuganiza, mwinamwake anthu twente sauzande. Ndipo iwo ali ndi mipingo ya Uthenga sikisite wani yathunthu imene yanena kuti ibwera ku msonkhano. Ndipo chotero ife tikuyembekezera nthawi yapamwamba kumeneko kwa masabata awiri.

Ambuye akudalitseni inu. Ndipo muzindipempherera ine, tsopano.

93 [M'bale Neville akuti, "Ine ndikungofuna kupanga cholengeza chaching'ono ichi, kuti ena a abale athu akukachotsa chogawa chipindacho, kumbuyo uko, usikuuno, zitheka kukhalamo anthu wani handiredi owonjezera, ine . . ." Malo opanda kanthu pa tepi. Osonkhana akuyimba, *Ine Ndikupita Ku Dzilo Lolonjezedwa*, pamene M'bale Branham ndi anthu akukonzekera ubatizo wa mmadzi. Pali malo opanda kanthu angapo pa tepi. Kuyankhulana ndi munthu aliyense sikunasiyanitsidwe chifukwa cha phokoso lapansi—Mkonzi].

94 . . .?. . .kusunga zinthu zonse zimene Inu munazilamulira. Pa. . .[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . .kudali-. . . [Malo opanda kanthu pa tepi.] . . .uyu, wanga m'ba-. . .[Malo opanda kanthu pa tepi]. . . .ndi kuvomereza kwake. . .[Malo opanda kanthu pa tepi.] . . .wa Ambuye Yesu, ndi wake wathunthu. . .?. . .[Malo opanda kanthu pa tepi].

95 (Lako ndi chiyani. . .?. . .Iwe ukhoza kudikira mpaka. . .?. . .aloleni iwo ayime pomwe apa. . .?. . .Oh, akuzizira, akuzizira kwambiri. . .?. . .Ife tiri ndi chinthucho apa. . .?. . .Dzina lako ndi ndani, mlongo? Ukuchokera kuti? Mwana wamkazi wa Opal Weaver. Um-hum. Amayi ako anapulumutsidwa ku imfa, si choncho iwo? Opal Weaver, iye anali ndi khansa. Uko nkulondola. Chabwino, iwe sungakhale namwino amene anali kumusi uko tsiku limenelo pamene ine ndinabwera pamenepo? Mmodzi wa ana ake aakazi ankaphunzira za unamwino. Eya. Pamene ine ndinapita kukamupempherera iye usiku umenewo kumeneko. . . Ziribwino. Akazi a Kennard, kodi inu munayamba mwabatizidwapo? Kukonkhedwa. Chabwino. Tsopano, mungoyang'ana uku. Izo ndi zabwino. Chabwino. . .?. . .Kodi amayi anu ali kunja uko?)

Awa ndi Akazi a Kennard. Ndipo kwa anthu amu mpingo pano, uyu ndi mwana wamkazi wa Mlongo Opal Weaver.

96 Ndipo nonse a inu mukumudziwa Opal Weaver, ndi chimene chinachitika mmoyo mwake. Iye anangotsala mafupa basi, anali ndi khansa, adokotala anali atamukanika iye. Ndipo Akazi a Weber oyandikana nawo, amene ali wachibale wawo, tsiku lina pamene ine ndinabwera kuchokera Kumadzulo, ku msonkhano, anandifunsa ine kuti ndipite kumusi kumeneko ndi kukawawona Akazi a Weaver. Akazi a Weaver anati, "M'bale Branham, ine sindiri woyenera kuti wantchito wa Khristu abwere mnyumba mwanga, chifukwa ndine wochimwa." Ndipo iye sanayankhule kwambiri za machiritso Auzimu, koma iye anayankhula za machimo ake. Iye sankafuna kuti adzakumane ndi Mulungu ali wochimwa. Ndipo pamenepo iye anapereka moyo wake kwa Mulungu. Ndipo anali. . .anabwera pa dziwe

ili, wodzandima ndi wolimba kwambiri, ali ndi miyendo ndi manja owonda, mpaka kuti iye ankawoneka ngati mafupa okha, anadzalowa mmadzi awa kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Iye wayima apo akulira tsopano, pamene iye akumuwonerera mwana wake akudutsa mu ubatizo womwewo umene iye analimo.

97 Kodi ndi inuyo, inu mwayima pamenepo, sichoncho inu, Akazi a Weaver? Inu mungasuntheko, kuti iwo awone mmene iye akuwonekera tsopano. Zaka zambiri zapitazo, anali mafupa a pafupifupi mapaundi forte. Ndipo uyu ndi mwana wawo wamkazi akulowa mu dziwe lomweli, mu Dzina la Yesu Khristu.

98 Mulungu akudalitseni inu, Mlongo Kennard. Inu mungoyika dzanja lanu mozungulira monga *chonchi*, Mlongo Kennard. Agwireni iwo kuzungulira anga. Chomwecho. Tsopano, izo ziri bwino, mungoyang'ana mmwamba mbali *iyi*. Tsopano tiyeni ife tiweramitse mitu yathu.

99 O Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka mphatso yabwino iliyonse. Pamene mkazi uyu wabwera mmawa uno, akuzindikira kuti Inu munawadzutsa amayi ake kuchoka ku mthunzi wa imfa, pamene iye anakumverani Inu mu ubatizo wa mmadzi, monga iye analonjezera pa bedi lake la imfa kuti iye akanadzatero. Iye akubwera mmawa uno, akudziwa kuti iye anangokonkhedwa, ndipo sanakhutitsidwe kuti umenewo unali ubatizo wa atumwi. Iye akubwera tsopano kuti akwaniritse chokhumba cha mtima wake ndi lamulo la Mulungu. Chotero, Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mumudzadze iye ndi Mzimu Woyera. Ndipo mumulole iye akhale moyo wautali, wokondwa, ndipo akhale wokutumikirani Inu.

100 Ndipo pa kuvomereza kwako kwa chikhulupiriro chako, ndi kudzipereka kwako kwa Ambuye wathu, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongoyo mmadzi—Mkonzi].

101 (. . .?. . .Tsopano, mubweretseni wina patsogolo panu, apa, kuti iwo awazolowere madziwa. Mwaona. . .?. . .Abweretseni iwo mozungulira. . .?. . .Bambo, bwerani mudzagwire dzanja lake. . .?. . .Abweretseni ena apa. Chabwino. Ine ndikufuna wina uja. . .?. . .Ndi zimenezo. . .?. . .Imani, imani pamenepo. . .?. . .Ndi zimenezo. Pamenepo, imani pamenepo. . .?. . .Belvin. Tsopano, mbweretseni mtsikana wina ndipo mumulole iye adzaime kumbuyo uko, akhoza kukhala akuwazolowera madziwa. . .?. . .muzikhala mukumubweretsa wina mmusi muno, azikhala akuwazolowerapo pang'ono iwo. Tsopano, muime mmbuyo mbali iyi, mlongo. Uko nkulondola. Chabwino, pamenepo. Belvin, wochokera ku Michigan. . .?. . .

chabwino. Ine ndikuganiza umu ndi mmene inu . . . ikani dzanja lanu pomwe apa. Chabwino.)

Mlongo Belvin, Maria, wochokera pafupi ndi Battle Creek, Michigan, amene wabwera kudzabatizidwanso mu Dzina la Ambuye Yesu.

102 Anthu, chifukwa chimene ife tinali onyinyirika pang'ono nthawi imeneyo, ngakhale kuti chotenthetsera chakhala chiri mmadzi awa kwa kanthawi, pansi pa dziweli pakuzizirabe mwa chipale. Ndipo ndi chifukwa chimene ife tikungowalola iwo kuti abwere, awazolowere madziwa.

Ndipo ine ndikuwafunsa iwo, kungowabweretsa iwo kuti iwo azingobwera mopitirira, mmodzi nthawi yonse.

Chotero tsopano ngati inu mungayike manja anu kuzungulira anga, Mlongo Belvin, monga *chonchi*, mupinde mikono yanu. Ndi choncho. Chabwino. Tsopano tiyeni tipemphere.

103 Atate Akumwamba, Wolungama kwambiri, Mwini wa Moyo wosatha, Wopereka mphatso yabwino iliyonse, mutumize madalitso Anu pa mkazi uyu amene wabwera njira yonse kuchokera ku Michigan, kuti adzatsatire Mwana Wanu mu ubatizo mmawa uno, mu dziwe lozizira ili. O Ambuye, imvani mapemphero a wantchito Wanu. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwudzadze moyo wake ndi Mphamvu Yanu, zinthu zabwino za Kumwamba. Ndipo, pamene ine ndikumubatiza iye ndi madzi, mudzadzeni iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu yokutumikirani Inu. Perekani izi, Mulungu Wamuyaya. Monga Inu mwatitumizira ife kuti tipite mu dziko lonse ndi kukapanga ophunzira a mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, kuwaphunzitsa iwo kuti asunge chirichonse chimene Inu munanena.

104 Chotero pa kuvomereza tchimo lanu, ndi chikhulupiriro chanu mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatizani inu, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongoyo mmadzi—Mkonzi].

105 (Dzina lako ndi ndani, huh? Joseph ndani? Blade? Dzina lake lomaliza ndi ndani? Chiyani? Blade. Chabwino. Ungoima mmusi uchoke apa, mwana, ngati iwe ungathe, chonde? Chabwino. Tsopano, iwe uyime apo, mlongo, kuchitira kuti . . . Ndi choncho. Chabwino.) Apa pali mnyamata wabwino, Joseph Blade. Mnyamata wamng'ono uyu wayimbapo zing'wenyeng'wenye mmbuyomu mochuluka ngati anthu handiredi ndi fifite sauzande. Iye adzakhala mlaliki wamng'ono. Ndipo iye wabwera kuti adzabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, osati mokakamizidwa ndi abambo ake, amayi ake, koma pa kukhudzika kwake iye wabwera. Iye akuyenera kukayimba ichi masana ano, kumtunda kuno kwinakwake mu Indiana;

koma amafuna kuti adikirire mpaka izi zitachitika, chifukwa iye wakhutitsidwa kuti izi ndi zolondola. Izo zinalembedwa Mmalemba, "Mwana wamng'ono adzazitsogolera izo." Tiyeni tiweramitse mitu yathu. (Gwira dzanja la M'bale Branham. Ndi momwemo, mnyamata, pomwe *apa*.) Tiyeni tipemphere.

106 Ambuye Mulungu, kunalembedwa, "Aloleni ana adze kwa Ine." Apa pali Joseph wamng'ono. Ine ndikamaganiza za dzina limenelo, ine ndimaganiza za mnyamata wanga wamng'ono. Ine ndikupemphera kuti Inu mumudalitse Joseph wamng'ono, mudzadze moyo wake ndi Mzimu Woyera, Ambuye. Mupangeni iye, mupatseni iye chokhumba cha mtima wake, muloleni iye adzakhale mlaliki wa Uthenga. Mupatseni iye kuchita bwino mu chirichonse chimene iye angachite. Ndipo pa kutuma Kwanu, Ambuye, monga Inu munatituma ife kuti tipite mu dziko lonse ndi kukapanga ophunzira, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera, ndi kuwaphunzitsa iwo kuti adzichita chirichonse chimene Inu munalamulira.

107 Ndipo pa kuvomereza kwa machimo a mnyamata uyu, ndi chikhulupiriro chake mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, m'bale wanga wamng'ono, Joseph, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza m'baleyo mmadzi—Mkonzi]. Ameni.

(Dzina lako ndi ndani, mlongo? Myers, Mlongo Myers. Oh, ndi Mlongo Downing apa, inu mukungobwera mmadzi.) Anthu awa akuchokera ku Tennessee.

108 Uyu ndi Mlongo Myers, wochokera ku Memphis, Tennessee, kuti akumane ndi Ambuye wake mu ubatizo mmawa uno. Ine ndikuganiza iwe unabatizidwapo kamodzi mu . . . ngati mwana. Ndipo iwe ukubwera tsopano kudzabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ngati iwe ungagwire dzanja langa, Mlongo Myers, ine ndikukhulupirira, ngati iwe ungatero mwina kutembenuza manja awiri onse. Ine ndikukhulupirira, donayo kanthawi kapitako . . . Ndi choncho. Ziri bwino. Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

109 O Ambuye Mulungu, Amene munaukitsa Yesu kwa akufa, ndipo mwatipatsa ife umboni mwa Mzimu Woyera, ife tayima apa mmanda achipale awa mmawa uno, podziwa ichi, kuti, motsimikiza monga Yesu anabwera kuchokera mmanda, ifenso tidzauka mu Tsiku limenelo. Tsiku lina, ngati Yesu achedwa, ife tidzapita ku—manda amatope, dothi lidzaponyedwa pa ife. Koma palibe manda amene angatigwire ife. Yesu anapereka lonjezo, "Iye amene akhulupirira ndi kubatizidwa, adzapulumutsidwa." Mkazi wamng'ono uyu akubwera lero, ndi mtima wodzipatula kwathunthu, akukhulupirira kuti Inu mumuchitira izi iye. Chotero, Ambuye Mulungu, Mlengi wa Kumwamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini wa Moyo wosatha,

tumizani madalitso Anu pa iye, pamene ine ndikukwaniritsa ntchito yanu imene Inu munatipatsa ife kuti tidziichita.

110 Pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chanu mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatizani inu, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongoyo mmadzi—Mkonzi]. Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

111 (Mlongo Downing ali pano. Bwerani kwa ine.) Uyu ndi Mlongo Downing, nayenso wochokera ku Memphis, Tennessee. Mulungu wakhala wabwino ku banja ili; mmene iye wa—wakhalira kwa amayi ake, amene akhala akudwala kwa nthawi yaitali. Uyu ndi mmodzi wa abwenzi apamtima a mkazi wanga. Ndipo iye akubwera lero, osati chifukwa chokakamizidwa, iye akubwera chifukwa chokhudzidwa, kuti akufuna kuti abatizidwenso mu Dzina la Yesu Khristu. Mulungu, mudalitseni mkazi uyu.

112 Ine ndikufuna kunena ichi. Ine ndingakonde kumupatsa munthu kaduwa kakang'ono pano, kusiyana ndi nkhata yonse iwo atapita. Ine ndamuwona mkazi uyu kwa zaka zambiri, chibwerereni ine mu utumiki. Ndipo mkazi uyu, podziwa mbiri yake, ya mmene iye wakhalira ndi chimene iye wachita; iye anali ndi mtima wodzadza ndi mavuto, koma iye wakhala mmodzi wa zitsanzo za Chikhristu. Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena izi mmawa uno. Ndipo iye ndi wopambana, kwa ine, monga Mkhristu wodzipatula. Ndine wokondwa kwambiri kuti ndikhoza kumunenera iye zimenezo, ine ndisanamubatize iye mu Dzina la Ambuye wake.

113 Mugwire manja awiri onse mmene inu mukufunira kuti muchite izo, Mlongo Downing. Pomwe apo zikhala bwino. Tsekani zala zanu monga *chonchi*, ine ndikukhulupirira izo zikupangitsani inu kuti mutulukemo bwino bwino.

114 Mulungu Wamphamvuzonse, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini mphatso iliyonse yabwino, ndi Mwini wa Moyo wosatha, Inu mwatituma ife kuti tipite mu dziko lonse ndi kukapanga ophunzira a mafuko onse. Ichi, Ambuye, ife tachipanga, molemekeza. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mumulandire mzimayi uyu, pa kukhudzidwa kwa mtima wake; iye poyamba atakhala ali mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Osati chifukwa choti ine ndanena izo; chifukwa chakuti iye watsimikizika kuti ndi Yanu yautumwi ndi njira Yanu yoyambirira yapachiyambi ya ubatizo, monga momwe Mpingo woyambirira unkabatizira. Iye akubwera monga—monga Paulo ananenera, wakale. Ndipo, Mulungu, ine—ine ndikupemphera kuti Inu mumulandire iye. Ndipo ine ndikudziwa kuti Inu mutero. Ndipo muwupanga moyo wake kukhala wokondwa tsopano. Mpatseni iye chokhumba cha mtima wake.

115 Ndipo pa kuvomereza kwa chikhulupiriro mwa Yesu Khristu, ndi pa kudzipereka kwanu kwa Iye, Ine ndikukubatizani inu, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi]. Ameni. Matamando akhale kwa Mulungu!

116 (Oh, ine ndikukhulupirira ndinu wotsatira, bwana, kuti mubwere. Dzina lanu ndi ndani? Henry Blade. Chabwino.) Uyu ndi Henry Blade, mnyamata amene wabwera kuti adzabatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Kodi iwe ndi mchimwene wa mnyamata wamng'ono amene wangobatizidwa kumene? Iwe umayimba zing'wenyeng'wenye, nawenso? Winanso wa gulu loyimba, amene amayimba zing'wenyeng'wenye, umaitanidwira kulikonse. Winawake amangondiuza ine kanthawi kapitako, kuti, iwo amayimba pamaso pa gulu lalikulu kulikonse. Ndipo iye wabwera chifukwa chokhudzika, kuti adzabatizidwe mu Dzina la Ambuye Wake wowukitsidwa. Kodi mungayende kubwera apa, M'bale Blade? Inu mungoyika manja awiri onsewo monga *chonchi*, kuzungulira nkono wanga. Ndi choncho. Tiyeni tipemphere.

117 O Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka wa mphatso yabwino iliyonse, tumizani madalitso Anu pa mnyamata uyu amene ine ndikumubatiza mu Dzina la Mwana Wanu. Perekani izi, Ambuye.

118 Pa kuvomereza machimo ako, ndi chikhulupiriro chako mwa Mwana wa Mulungu, Ine ndikukubatiza iwe, m'bale wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza m'bale mmadzi—Mkonzi]. Chabwino, mnyamata wamng'ono ameneyo, mudalitseni iye!

(Dzina lako ndi ndani? Chiyani? Myers.) Uyu ndi M'bale Myers wamng'ono. Iwe uli ndi zaka zingati? Teni.

Winawake akhoza kunena kuti, "Nchifukwa chiyani mukumubatiza mnyamata wamng'ono uyu?"

119 Yesu anati, "Aloleni ana aang'ono abwere kwa Ine, musawakanize iwo ayi, pakuti Ufumu wa Mulungu uli monga oterewa." Aloleni iwo kuti abwere! Mnyamata wamng'ono uyu akufuna kuti abatizidwe. Ine ndikukhulupirira iwo anachita kutuluka ndi kukamutengera iye zovala, kapena chinachake, kuti abatizidwe. Iye wakhutitsidwa. Tiyeni tipemphere.

120 Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka mphatso yabwino iliyonse, tumizani Madalitso Anu pa mwana uyu, amene akubwera kwa Inu mmawa uno, mmanda achipale awa. Pamene ine ndikumubatiza iye ndi madzi, mudzadzeni iye ndi Mzimu Woyera.

121 Pa kuvomereza kwa machimo ake, ndi chikhulupiriro chake mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, m'bale wanga wamng'ono, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza m'baleyo mmadzi—Mkonzi]. Dalitsani mtima wake waung'ono!

122 (Chabwino, Mlongo Ungren.) Dona uyu apa, wakhala ali chikho cha chisomo cha Mulungu. Uyu ndi bambo . . . Akazi a Ungren, amake a mtsikana wa a Downing ndi mtsikana amene anali pambuyo pake, amene wangobatizidwa kumene. Iwo onse akuchokera ku Memphis, Tennessee. Uyu wakhala ali mzathu kwa zaka ndi zaka. Ndipo iye akuchokera ku mpingo wa utatu kumusi mu Memphis, Tennessee. Ine sindingamuuze Mlongo Ungren kapena aliyense kuti asamapite ku tchalitchi. Ndithudi, inu muzipita ku tchalitchi chanu chomwe. Izo nzabwino. Koma, iye sakuchita izo chifukwa chakuti ali ndi chinachake chotsutsana ndi tchalitchi chake, iye akuchita izi chifukwa watsimikizika ndi Uthenga kuti uwu ndi ubatizo wa utumwi. Mulungu akudalitseni inu, Mlongo Ungren. Iye wakhala akudwala, akudutsa mu nthawi ya moyo, izo sizinamuchitire iye ubwino uliwonse.

123 Ndipo Mlongo Weaver, pamene inu mukuyima apa, ndi mboni yakuti zimenezo . . . Ndipo ambiri a inu pano amene mukudziwa zimenezo, pamene inu munabatizidwa kenanso mu Dzina la Yesu Khristu. Ena a inu kunja kumeneko munali ndi khansa ndipo simumakhoza kuchira; pamene inu munadzabatizidwanso mu Dzina la Yesu, khansayo inakuchokerani inu. Akazi a Weaver ndi mmodzi wa iwo. Ndipo dona kutsidya kwa msewu kumeneko ndi mmodzi wa iwo, amene zinawachitikira zimenezo.

Ndipo ine ndikudalira Mulungu kuti awa akhala mapeto a kuvutika kwako, mlongo, chifukwa iwe wamvera Malamulo a Mulungu.

Tsopano ngati inu mungayike manja anu mozungulira anga, basi mulimonse mmene inu mukufunira kuwagwira iwo. Tiyeni tipemphere. Chabwino.

124 Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, apa payima wantchito Wanu, ndipo iye wakhala akudwala kwa kanthawi, koma, O Ambuye, iye wayima apa lero mu dziwe ili, kuti adzabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Ambuye, ine ndawakonda anthu awa, ndipo ndawapempherera iwo mowirikiza, kuti iwo adzawone Kuwala kwakukulu uku. Pakuti, ine ndikukhulupirira, Ambuye, ndi zimenezo, mtima wanga wonse, ndi mmene Inu munatidzodzera ife kuti tizipita. Ine ndikupemphera kuti Inu mumuchiritse Mlongo Ungren tsopano. Mulole dontho lirilonse la matenda lisiyidwe mu dziwe ili. Mulole iye adzuke mu thanzi latsopano, ndi mu mphamvu ya chiukitsiro cha Khristu.

125 Pa umboni wake ndi kuvomereza kwake, ndi chikhulupiriro chake mu Mawu a Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi].

126 (Chabwino, m'bale. Ine ndikukhulupirira iwe ndi wokonza mawayilesi, sichoncho iwe, kapena chinachake? Mwamuna waku wayilesi. Kodi iwe ungatembenuke ndi kuyima? Dzina lako ndi ndani? Bert Maine. Ngati iwe ungatembenuke... Eya.) Uyu ndi M'bale Bert Maine, mwamuna waku wayilesi, mwamuna wa nkhani, wolengeza nkhani za steshoni ya wayilesi, amene wakhutitsidwa kuti ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu Khristu ndi woona. Kodi iwe unabatizidwapo, m'bale? Iye anabatizidwapo, mu dzina la "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Koma wakhutisidwa ndi kuwerenga kwa Mawu, kuti ichi ndi chimene iye akuyenera kuchita. Mwamuna waudindo wake ndi ntchito yake, akubwera molunjika ku madzi, kufuna kuti Mulungu amudalitse iye ndi kumupatsa iye chimene Iye ali nacho cha iye mmoyo. Mulungu adalitse wantchito Wake wokhulupirira uyu.

Ingoyenda kubwera kuno, M'bale Bert, uyike manja awiri onse mozungulira anga, awa pomwe apa. Ndi zimenezotu. Tiyeni tipemphere.

127 Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka mphatso yabwino iliyonse, tumizani madalitso Anu pa m'bale uyu. Ndipo pamene iye akubwera apa ngati mboni ya chisomo Chanu, wowerenga Mawu Anu, wakhutitsidwa mu mtima mwake kuti ichi ndi chinthu choti achite, chifukwa ndi kutuma kwa Mpingo Wanu woyera. Icho ndi chapachiyambi. Ndipo, Ambuye, ife tikufuna titsatire Malamulo a iwo amene akuyenda ndi Inu, pakuti moonadi chokhumba chathu kuti tiyende monga momwe iwo anayendera, titenge njira imene atumwi anayiyenda. Mwinamwake mazunzo, mwinamwake kupweteka mtima kwake, mwinamwake zisoni zake, ife sitikudziwa chimene icho chiri nazo, koma, Ambuye, koma ngati Inu mukutsogolera, ife tikudziwa izo zikhala bwino. Dalitsani m'bale wathu, dzadzani moyo wake ndi Mzimu Woyera, ndipo adzipatulire iyemwini ku utumiki wa Khristu.

128 Chotero, pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chanu, ndi kukhutisidwa kwanu kwa ichi chimene inu mukukonzekera kuti muchichite tsopano, m'bale wanga wokondedwa, ine ndikukubatizani inu mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza m'bale mmadzi—Mkonzi].

129 (Ndinu Mlongo...Mlongo Skaggs. Kodi ndinu mwana wamkazi wa M'bale Skaggs apa, mzanga? wochokera a...wochokera...?...) Uyu ndi Mlongo Skaggs. Inu munabatizidwapo, Mlongo Skaggs? Munabatizidwapo kale,

mu "Atate, Mwana, Mzimu Woyera." Iye akubwera mmawa uno, mkazi wamng'ono uyu, kuti adzapereke moyo wake wa kudzipatula kwa Ambuye Yesu, kuti amutsatire Iye mu ubatizo wa utumwi. Ambuye akudalitseni inu, Mlongo Skaggs. Inu mungabwere mbali iyi moyandikira pang'ono? Muyike manja anu basi mulimonse mmene inu mungafunire kuti mugwire anga. Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

130 Mulungu wamphamvuzonse, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini Moyo wosatha, ndi Wopereka wa mphatso iliyonse yabwino, tumizani madalitso Anu pa mdzakazi Wanu wamng'ono uyu. Ine ndikupemphera kuti Inu mudzadze moyo wake ndi zifundo ndi madalitso a Mulungu, akupatulira solo yake kwa Inu, Ambuye, ndipo mudzadzeni iye ndi Mzimu Wanu ndi chikondi.

131 Pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chanu, mlongo wanga wokondedwa, ine ndikukubatizani inu mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi]. Ameni.

132 [Winawake akufunsa za winawake—Mkonzi]. (Chirichonse chimene iye ali, ngati iye wakhutitsidwa, chabwino, chabwino ndiye. Chabwino. Dzina lanu ndi ndani, tsopano?) Uyu ndi M'bale Henry B. Johnson. Iye anabwera kuno Isitara yapitayo kuti adzabatizidwe, ndipo analibe zovala zake, ndipo iye wadikira kwa chaka kuti adzabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Mulungu mudalitse wantchito wochirimika wa Khristu uyu! Yendani mubwere pomwe apa, M'bale Johnson. Ingoyikani manja anu mozungulira anga apa, mulimonse mmene inu mukuganizira kuti mungathe kuzidzutsa nokha mwabwinoko. Ndi chonchotu. Ndi choncho. Tiyeni, tipemphere.

133 Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini Moyo wosatha, Wopereka wa mphatso yabwino iliyonse, tumizani madalitso Anu pa mtima wodikirira uwu. Oh, pamene Inu mukumuwona iye akubwera kuchokera mmadzi awa, mulole Mzimu Woyera umene unkayenda pa madzi chinthu choyamba, mulole Iwo uyenderere pa iye. Apatulire moyo wake, O Mulungu, kwa Inu, utumiki.

134 Pa kuvomereza kwa machimo anu, ndi chikhulupiriro chanu mwa Yesu Khristu, ine ndikukubatiza iwe, m'bale wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. [M'bale Branham akumumiza m'bale mmadzi—Mkonzi]. Mulungu alemekezeke!

135 (. . .?. . .iwenso. Kuzizira? um-hum. Tiyeni tiwone, chiyani. . .? Martha, ndi choncho? Kapena, Jo Ann.) Uyu ndi mtsikana wina wochokera kwa mmodzi wa. . .mwana wamkazi wa Mlongo Downing, Jo Ann Downing wamng'ono. (Uko nkulondola, mlongo? Iwe uli ndi zaka zingati pano? Fortini.) Iye ndi—ndi bwenzi wapadera wa mtsikana wanga,

Rebekah, wayima apa akumuwona iye akubatizidwa, mu Dzina la Ambuye Yesu. Ndife okondwa kwambiri lero kumuwona Jo Ann wamng'ono, pa kukhudzika, ana a zaka zammatini awa, pamene dziko ili ladzadza ndi tchimo ndi chivundi, kuwawona iwo akupanga kusankha kwawo ndi Yesu Khristu. Mulungu adalitse mtsikana wamng'ono uyu. (Pamene iwe ukugwira manja ako.) Tiyeni tipemphere.

136 Mulungu wamphamvuzonse, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini wa Moyo wosatha, tumizani madalitso Anu pa mzimayi wamng'ono uyu. Pamene ine ndikumubatiza iye ndi madzi, ine ndikupemphera kuti Inu mudzamudzadze iye ndi Mzimu Woyera. Mupereke kuti moyo wake waung'ono ukhale a—mdalitso kwa Inu, Ambuye. Perekani izi. Ndipo muyankhule naye iye, ndipo mukhale mwa iye ndi kugwira ntchito kudzera mwa iye, Ambuye, kudzera mu Mphamvu ya Mulungu.

137 Pa kuvomereza kwako kwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi].

138 (Chabwino, Mlongo. Amayi ako ali apa? Eya. Akuzizirira iwe. Dzina lako ndi ndani? Sharon Myers, yang'ana mbali iyi, Sharon.) Sharon Myers, mkazi wina wamng'ono akubwera tsopano, akudzapereka moyo wake kwa Khristu. Kodi iwe unayamba wabatizidwapo, Sharon? Ayi, iyi ndi nthawi yake yoyamba kuti abatizidwe. Ambuye adalitse mkazi wamng'ono uyu, ndipo adzadze moyo wake ndi ubwino wa Mulungu ndi chifundo.

139 Ingobwera kumtunda kuno, Mlongo Sharon. Ndipo udzangoyika manja awiri onse monga chonchi, ine ndikukhulupirira, pansi mbali *iyi* zingakhale bwino. Basi mulimonse mmene iwe ungagwirire iwo tsopano monga choncho, chabwino, Mlongo Sharon. Tiyeni tipemphere.

140 Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka mphatso yabwino iliyonse, tumizani zifundo Zanu pa mlongo wathu apa. Ndipo mulole iye akhale moyo ndipo akhale chitsanzo cha—cha Chikhristu chenicheni, mwa oyandikana nawo kumene iye akuchokera. Perekani izi, Atate. Ndipo monga Inu mwatituma ife kuti "pitani mdziko lonse lapansi ndipo mukaphunzitse mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera," kuwaphunzitsa iwo kuti azichita chirichonse chimene Inu mwatilamulira ife. Perekani izi, Ambuye, kuti mtsikana wamng'ono uyu alandire madalitso amene Inu munalonjeza.

141 Pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chako, ndi—ndi pa kudzipereka kwako kwa Mwana wa Mulungu, Ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina

la Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi].

142 (Tsopano, nsapato siziri . . . Eya, sutukesi ija ya zovala zonyowa. Um-hum. Chabwino. Ndipo dzina lanu ndi? Sumner. Yang'anani kuno.) M'bale Sumner. Inu mukuchokera kuti, M'bale Sumner? Kuchokera kumusi ku Georgia, iye wabwera mmawa uno. Inu munabatizidwapo, M'bale Sumner? Iye anabatizidwapo, "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Wakhutitsidwa kuti ichi ndi Choonadi, iye wabwera mmawa uno kuchokera komwe uko ku Georgia, kuti adzabatizidwe kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu, pa mmawa wa Isitara uwu, akuvomereza chikhulupiriro chake mwa Mwana wa Mulungu. Inu musunthire mbali iyi, M'bale Sumner, ndipo muyike manja anu mozungulira anga. Tiyeni tipemphere.

143 Ambuye Mulungu, pamene ine ndikumubatiza iye ndi madzi, ine ndikupemphera kuti Inu mumudzadze iye ndi Mzimu Woyera ndi Moto. Mnyamata uyu, moyo wopatulika, Ambuye, mutumizeni iye kunja mu minda ya umishonare kwinakwake, kuti akagwire ntchito Yanu.

144 Ndipo pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chake mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, m'bale wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza m'bale mmadzi—Mkonzi]. Mulungu akudalitse iwe, m'bale wanga wolimba.

145 (Iwe ndi mlongo . . . [Mlongo akuti, "Sumner."—Mkonzi]. Uyo ndi mwamuna wako? ["Inde."] Chabwino, ndizabwino bwanji! Ine ndidalira kuti Mulungu a—adalitsa.) Uyu ndi mlongo Sumner, inu mukumvetsa. Uyo anali mwamuna wake amene wangobatizidwa mphindi zingapo zapitazo. Ife tikuwalora anthu kuti ayime kwa maminiti ochepa, kuti iwo awazolowere madziwo. Chabwino, Mlongo Sumner, ngati inu mungayike mikono yanu mozungulira yanga. Ine ndikukhulupirira ngati inu mungaisemphanitse monga *chonchi,* Mlongo Sumner, izo zingakhale bwino. Tiyeni tipemphere.

146 Ambuye Mulungu, monga Mlongo Sumner akubwera tsopano mo—motsatira mu ubatizo, Ambuye wathu ndi Mpulumutsi. Akubwera motsatizana ndi mwamuna wake, zoyenera bwanji! Ine sindinadziwe zimenezo. Koma kudikira mpaka nthawi imeneyo, chimenechi chikuyenera kukhala chifuniro Chanu chodzozedweratu, Ambuye, ndi njira Yanu yochitira zinthu, kuti iye akhoze kumutsatira mwamuna wake, nayenso, pakuti iye ndi chitsanzo kwa iye. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mumudalitse iye ndi kupatula moyo wake. Ndipo mulole iwo akakhale moyo wautali, miyoyo yokondwa limodzi, akuwalera ana awo ndi kukutumikirani Inu. Pamene iye akubwera tsopano kuti adzabatizidwe, ine

ndikupemphera kuti Inu mumupatse iye chokhumba cha mtima wake.

147 Pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chako mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi].

148 (Nthawi yoyamba imene inu munabatizidwapo, Mlongo Sothmann?) Uyu ndi mmodzi wa mkazi wa mzanga wapamtima, M'bale Fred Sothmann wochokera ku Hughton, Saskatchewan, Canada. Mlongo Sothmann, iye ndi munthu wokondeka kwambiri, mzimayi wopatulika, mayi weniweni, mkazi weniweni ndi wokondeka wa mzanga, Fred. Ine ndikupemphera kuti Mulungu adalitse Mlongo Sothmann, ndipo amupatse iye mphatso iliyonse ya Ufumu imene iye akuyifuna.

149 Inu mukhoza kuyika dzanja lanu pomwe apa. Ine ndikukhulupirira ichi chingakhale chapamwamba, Mlongo Sothmann, muliyike ilo monga *chonchi*. Kenako ili pansi, monga *choncho*. Tiyeni tipemphere.

150 O Ambuye Mulungu, Mlengi wa Kumwamba ndi dziko lapansi, ine ndi wotsimikiza basi kuti Inu mwayima penapake pamalo ano pano mmawa uno, mukuyang'ana pa ichi, pakuti palibe munthu angachite chirichonse mu Dzina Lanu popanda Inu kudziwa za izo. Inu mukuona chikhulupiriro cha mzimayi uyu ndi kudzipatula kwake. Ine ndikupemphera kuti inu mumudalitse iye ndi M'bale Fred, palimodzi, mulole iwo akakhale moyo wautali, wosangalala, akukutumikirani Inu. Perekani izi, Ambuye. Ndipo pamene iye wabwera tsopano ndi mtima wodzipereka kwathunthu, ndi kudzipatula, kuti abatizidwe mogwirizana ndi mmene atumwi ankabatizidwira, mmene iwo ankabatizira.

151 Chotero, pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chake mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi].

152 (Zikukhala ngati ukunjenjemera? Dzina lako ndi ndani? Hudgins.) Mlongo Doris Hudgins. Iwe wachokera kuti, Mlongo Hudgins? New Albany. Iye wabwera mmawa uno kuti adzabatizidwe mu Dzina la Mpulumutsi wake. Ambuye Mulungu wa Kumwamba amudalitse iye ndipo amupange iye kukhala mdalitso mu New Albany, kumene iye ati abwerere.

153 Ikani—ikani dzanja ili pansi monga *chonchi*, kumbuyo. Chabwino. Musiyeni mwanayo pomwepo kwa kamphindi chabe, mpaka ine nditamubatiza iye. Iwo ndi ozizira kwambiri kwa mtsikana wamng'ono. Kodi uyu ndi mchemwali wanu wamng'ono? Oh, izo ndi zopambana kwambiri. Mphindi chabe, ife tisamalira zimenezo. Tiyeni tipemphere, mutero inu?

154 Mulungu wamphamvuzonse, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka wa mphatso zonse zauzimu ndi zathupi, mupereke kwa mkazi uyu thanzi labwino, mphamvu, chisangalalo, ndi madalitso onse auzimu amene Inu mwamusungira iye. Inu simukufuna kuti ife tizisowa mu chirichonse. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izi, Ambuye, kwa iye, pamene iye akudzipatula yekha, pokutsatirani Inu ku manda ozizira awa mmawa uno. Mulungu, perekani izi.

155 Ndipo pa kuvomereza kwa chikhulupiriro chako, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi]. Mulungu alemekezeke! . . .?. . .

156 (Ndipo iwe, kodi iwe ukuwazolowera iwo? Iye akhoza kukhala ndi mantha pang'ono ndi iwo. Dzina lako ndi ndani, wokondedwa? Blade? Kodi iwe ndi. . . abale ako angobatizidwa kumene?) Mary Alice Blade wamng'ono. Iwe uli ndi zaka zingati, wokondedwa? Usinkhu wa zaka leveni. Ambuye adalitse mwana uyu, apereke kwa iye kuwona mtima ndi chikhumbo, chokhumba choona cha mtima wake, ndiro pemphero langa. Iwe ungabwere kuno. Mary Ellen? Mary Alice. Uh-huh. Chabwino, bwana. Tiyeni tipemphere.

157 Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka wa mphatso yabwino iliyonse, tumizani madalitso Anu pa mwana uyu apa, pa nthawi ya kusintha kwa moyo. Mulole ife, iye apitirize pa njira iyi yolowera ku Moyo. Perekani izi. Pamene iye wabwera mmawa uno, akuvomereza machimo ake, ndi kuvomereza kuti iye ali ndi chikhulupiriro mwa Yesu Khristu Amene anafa kuti amupulumutse iye ku machimo amenewo, iye akulowa mu dziwe lozizira ili, kuti adzabatizidwe mu Dzina la Mpulumutsi wake. Perekani, Ambuye, kuti Mzimu Woyera ukhale ukuyenda pa madzi pamene iye akubwera pano, ndipo muyende mu mtima wake, ndipo musamusiye konse iye, kuyambira lero mpaka Muyaya yense. Perekani izi, Ambuye.

158 Pa kuvomereza kwa machimo ako, ndi chikhulupiriro chako mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi].

159 (Chabwino, bwana. Iwe sungayime motalikirapo pang'ono ndi kundilola ine nditenge wina apa. Kodi uyo. . . aliponso ena akubwera kudzabatizidwa? Iwe ukufuna kuti ubatizidwe, mlongo? Chabwino. Iwe ukubwera, wokondedwa, kuti udzabatizidwe? Mtsikana wina wamng'onoyo akubwera nayenso? Chabwino. Aloleni iwo azizolowera iwo pang'ono, aloleni iwo azipita mwakachetechete basi, izo zikhala bwino, mungoyima modekha kwenikweni. Ndipo mungolola mtsikana

wamng'onoyo angoyenda, ayende sitepe imodzi pa nthawi, pamene iye akubwera. Ungoyima pamenepo, tsopano, pang'ono. Ndipo mulole winayo achite zimenezo. Dzina lako ndi ndani, mlongo? Dorothy ndani? Darlene. Chabwino, iwe ukuchokera kuti, Darlene? Kumusi mu Kentucky.) Uyu ndi Darlene Wilcoxson wamng'ono, wochokera ku Kentucky. Iye wabwera mmawa uno, mu kuvomereza kwa chikhulupiriro mwa Mwana wa Mulungu, kuti adzabatizidwe mu Dzina la Ambuye wathu ndi Mpulumutsi, Yesu Khristu. Mulungu amudalitse iye. Ine ndimakonda kuwawona ana a zaka zammatini akubwera, chifukwa, ngati kuli mawa, awa adzakhala ogwira antchito a mawa. Ndipo, molondola, dona wokondedwa wamng'ono, pa zaka zimene Satana akhoza kuyamwa moyo wake ndi kumupanga iye kukhala cha—chamanyazi. Iye watenga njira yolondola. Khala pa iyo, Darlene, mpaka Yesu adzakumasule iwe. Ungoyika dzanja limodzi monga *chonchi*. Ndipo, ine ndikukhulupirira, Darlene, monga *chonchi,* wokondedwa, ndipo kenako pamwamba monga *choncho*. Izo ziri bwino. Tiyeni ife tipemphere.

160 Mulungu wachifundo, Amene munalenga Miyamba ndi dziko lapansi, ndipo munapereka zinthu zonse mwaulere kudzera mwa Yesu Khristu, ife tikukuthokozani Inu mmawa uno chifukwa cha mwayi umene ife tiri nawo owatsogolera ana awa kwa Inu. O Mulungu wachisomo, dzadzani moyo waung'ono uwu. Ndipo musalole kuti mdierekezi amugwire iye! Mulole iye adzakhale wantchito Wanu masiku onse a moyo wake. Perekani izi, Ambuye. Monga iye wayambapo mmawa muja, atayima mmanda ozizira awa, akupita kumusi kuno, akukhulupirira kuti Yesu Khristu anafera machimo ake, ndipo iye akupanga kuvomereza kwa pagulu kwa izo tsopano. Musalembe dzina lake pa pepala la ubatizo lokha, koma ilo likhale mu Bukhu la Moyo. Mulole iye adzabwere patsogolo mu tsiku limenelo, akuwala ngati golide. Perekani izi.

161 Pa kuvomereza kwa machimo ako, ndi chikhulupiriro chako mwa Mwana wa Mulungu, Ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi].

162 (Chabwino. Dzina lako ndi ndani? Emily . . . ? Plade.) Ndi mtsikana wokoma bwanji uyu, Emily Plade wamng'ono. Ndi chikhulupiriro chanji . . . [Winawake akuti, "Blade."—Mkonzi.] Blade. Oh, iwe ndi . . . mmodzi wa . . . Ujayu anali mlongo wako amene wangobatizidwa, iye ndi wokondeka wamng'ono.

Bwanji, winawake ananena kwa ine nthawi ina, anati, "M'bale Branham, nchifukwa chiyani inu mumabatiza ana?"

Yesu anati, "Lolani ana adze kwa Ine." Uko ndikuti, *lolani*, "aloleni" iwo abwere.

Kuti, "Chabwino, iye sakudziwa chimene iye akuchita."

163 Iye akhoza kudziwa ngati iye wachita cholakwika, iye sangatero? Iwe ukuganiza kuti mwana ameneyo sangadziwe pamene iye wachita cholakwika? Ngati iye ali wamkulu mokwanira kudziwa pamene iye walakwitsa, iye ndi wamkulu mokwanira kuti adziwe pamene iye wachita molondola. Nanga bwanji ngati chinachake chitachitika kwa iye, ndipo ine ndinamuletsa iye? Ndiye, magazi amenewo akhoza kukhala mmanja mwanga pa Tsiku la Chiweruzo. Inde, bwana. Ziribe kanthu iwo ali ndi zaka zingati pamene inu . . . pamene iwo akufuna kubwera, inu mudziwalola iwo kuti abwere.

164 Inu mumamukonda Yesu? Inu mukamutumikira Iye? Inu mukudziwa chimene dziwe ili liri mmawa uno? Pamenepo ndi pamene Iye anafera, anaikidwa, pansi mmanda ozizira kwenikweni awa; koma Iye anaukanso, Mulungu anamuukitsa Iye. Tsiku lina, wokondedwa, iwe udzaukanso, nawenso. Iwe umukonde Yesu, ndipo uzikamutumikira Iye masiku onse a moyo wako. Tsopano tiyeni tipemphere.

165 Ambuye, kunalembedwa, "Lolani ana adze kwa Ine, ndipo musawaletse iwo, pakuti Ufumu wa Mulungu uli wa oterewa." Ine ndikupemphera kuti Inu mumudalitse mwana uyu. Pamene ine ndikumubatiza iye ndi madzi, ndipo Inu mumubatize iye ndi Mzimu, Ambuye. Iye wabwera, iye akukhulupirira, iye wabwera mwa chifuniro chake chomwe. Ndipo ine ndikumubatiza iye mogwirizana ndi Mawu Anu.

166 Pa kuvomereza kwa machimo ake, ndi chikhulupiriro chake mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—Mkonzi].

167 (Kodi zikukuyendera bwanji? kodi zikukuyendera bwanji, wokondedwa, ziri bwino? Dzina lako ndi ndani? Chabwino. Dobson? Robison.) Uyu, ndi mlongo wamng'ono Robison amene wabwera kuti adzamizidwe mu Dzina la Mpulumutsi wake, Ambuye Yesu. Tiyeni, tiweramitse mitu yathu tsopano pamene ife tikupemphera. Ika manja ako pomwe *apa*, wokondedwa.

168 O Ambuye Mulungu, Mlengi wa Miyamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini wa Moyo wosatha, ndi Wopereka wa mphatso yabwino iliyonse, tumizani madalitso Anu pa dona wamng'onoyu. Pamene iye akubwera mmawa uno akudzavomereza machimo ake, ndi kumakhulupirira mwa Mwana wa Mulungu, perekani, Ambuye, kuti iye adzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Ndipo mulole iye atenge msewu wolondola, ndipo apitirire pa iwo, mpaka iye adzakhale mfulu ku moyo uno. Perekani izi, Ambuye. Mupatseni iye madalitso a moyo wake.

169 Tsopano, pa kuvomereza kwa machimo ako, ndi chikhulupiriro chako mwa Mwana wa Mulungu, ine ndikukubatiza iwe, mlongo wanga wokondedwa, mu Dzina

la Yesu Khristu. Ameni. [M'bale Branham akumumiza mlongo mmadzi—mkonzi]. Ameni. Ameni. Ambuye alemekezeke!

170 (Sabata likubwerali. Inde. Iwe ukuwopa pang'ono kuti ubwere pano, wokondedwa? Huh? Amayi ali kuti? Uh-huh. Kodi iwe ukuganiza chiyani, iwe ukufuna uyesere izo? [Amayi akuti, "Chabwino, izo ziri kwa iye. Iye wakhala akundipempha ine, ndipo ine ndayesera kumuletsa iye za izo."—Mkonzi]. Iwe ukufuna kuti ubatizidwe, wokondedwa? Ndithudi? Inu ukufuna kutero, wokondedwa? Ukufuna kulowa mmadzi ndi M'bale Branham? Iwe ukuwopa kutulukamo? Huh? Iwe ukufuna kubwera, wokondedwa? Iwe ukufuna—iwe ukufuna, bwera kuno? Chabwino, mlongo, izo zikhoza kukhala zopereka mantha kwa iye pang'ono. Mupatseni iye chimenecho. Tsopano, alipo—alipo winawakenso mmenemo? Amene . . . Alipo winawakenso mbali iyi? Chabwino, kokani chophimba pamenepo. Um-hum. Chabwino.) Mtsikana amene anayima pano tsopano kuti abatizidwe, iye amafuna kuti abatizidwe, koma iye amawopa kuti madzi anali ozizira kwambiri kwa iye. Ndipo chotero amayi ake anati . . . Chabwino, iye anandifunsa ine chimene ine ndimaganiza. Ine ndinati, "Mwinamwake ngati iye akuwopa, ine sindingafune kuti ndimuwopsyeze iye." Mukuona? Ndipo iye anali wamng'ono kwambiri, ndiponso. Koma iye akukamba zakuti akufuna kuti abatizidwe, chotero iye anaganiza kuti adikirira mpaka ubatizo wotsatira, mwina madzi adzakhala otentha pang'ono. Chotero izo ndi zokoma kwenikweni, ndi amayi ake. Ndipo ife tikupemphera kuti Mulungu . . .

Tiyeni timupempherere mtsikana wamng'onoyu.

171 Ambuye Yesu, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha chinthu chaching'ono chimenecho. Ndipo icho ndi . . . Icho chikhale chidzudzulo kwa anthu aakulu, poona kuti, pamene mtima waung'ono umenewo uli wanthete ndi waung'ono, iye akufuna kuti abwere. Wochepa kwambiri, Ambuye, zikuonetsa kuti Inu mumachita ndi mtima pamene iwo wabwera modzichepetsa ndi mophweka. Mulole icho chikhale chitsanzo, Ambuye, kuti Inu mukhoza kuchita ndi anthu. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mukhale ndi mtsikana wamng'onoyo, ndipo mumuthandize iye. Mulole iye akule, ndi wamphamvu ndi kukula, mpaka iye adzabatizidwe mu Dzina la Mwana Wanu. Perekani izo, Atate.

172 Ndipo tsopano kwa awa, Atate Mulungu, amene abatizidwa, pamene ine ndidakali muno mmadzi. Ndipo Wanu—Mzimu Wanu wakhala uli pano; ife tinawaona atsikana awa akudzuka, ndi anyamata, ndi manja awo mmwamba, akukulemekezani Inu. Ife ndi oyamikira kwambiri chifukwa cha izi, kudziwa kuti Mzimu Woyera uli pafupi. Dalitsani, Ambuye. Adalitseni iwo amene akhala akudikirira, abambo ndi amayi, okondedwawo, amuna, ana aakazi, a—amayi, ndi ena onse. Ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo onse.

173 Ndipo tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mutipatsa ife mpumulo masana uno. Ndipo mundithandize ine pamene ndikupita mu mzere wa kuzindikira zamumtima masana ano ndi usikuuno, kuti Mzimu Woyera u. . . Titatha kuchita zinthu izi, mulole izo zikhale chipambano chachikulu chimene ife tinayamba takhalapo nacho mu kachisi, usikuuno. Mulole pakhale mphamvu yosaneneka, muno mu kachisi, yoti ichiritse odwala onse ndi osautsika. Perekani izo, Ambuye.

174 Tikupemphera ndi kudzipatula tokha. Ndipo ine ndayima pano mu awa, manda amadzi awa mmawa uno, ine ndikudzipatulira ndekha kachiwiri kwa Inu, Ambuye. O Mulungu, ngati muli chirichonse mwa ine chimene Inu mungachigwiritse ntchito, chitengeni icho. M'bale Neville, ndi tonse a ife pamodzi, monga atumiki, kapena madikoni, monga ogwira nawo ntchito mu Uthenga, ife tikudzipatulira tokha kwa Inu, O Mulungu. Tigwiritseni ntchito ife, Ambuye. Tipatseni ife chiwukitsiro chatsopano mu mtima mwathu, mwa chotichitikira. Titumeni ife kunjako, tiri odzozedwa ndi Mzimu Woyera, kuti tikhoze kuchita ntchito ya Mulungu wamoyo. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

Msonkhano ndi wanu, M'bale Neville.

Ubatizo Wa M'madzi CHA59-0329M
(Water Baptism)
Maulaliki a Isitara

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi pa Isitara Lamlungu mmawa, Marichi 29, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org